BUKHU

[LOMASULIRIDWA]

LA

CHIVUMBULUTSO

BUKHU 3
[CHAPUTALA 9–13]

Kwa
Mkwatibwi wa Khristu
Bukhu ili laperekedwa

BUKHU {LOMASULIRIDWA} LA CHIVUMBULUTSO

BEN HOWARD

Translanted To Chichewa Language
By
Enoch Kamanula
New Testament Assembly
P.O. Box 64
Mwanza-Malawi

KUSINDIKIZIDWA KOYAMBA 1980

KUSINDIKIZIDWA KACHIWIRI 2005

Palibe gawo la bukhu ili limene lingachulukitsidwe [kupatula lemba la Baibulo] popanda chilolezo cholembedwa. Kuti mumve zambiri lemberani ku:

Sound of Liberty
Ben Howard
7286 Hwy 53W
Dawsonville, Georgia 30534 (USA)
TwoAnds@soundofliberty.org
www.SoundofLiberty.org

MALONJE

Bukhu la Chivumbulutso ndi bukhu la zoimirira, limene; politanthauzira, ndi uneneri wapamwamba. Ili si bukhu limene likuchita ndi chiphunzitso kapena ziphunzitso za maziko zimene zinabwera kwa ife ndi mtumwi Paulo ndi alembi ena a malemba za m'mene tingapulumutsidwire kapena m'mene tingalandirire dongosolo la chipulumutso la Mulungu.

Bukhu la Chivumbulutso linalembedwa mu 96 A.D. mpingo utagwa ku chikondi chake choyamba. [Chivumbulutso 2:4] Chikuonetsa m'mene mpingo unathera kudutsa mu nthawi mu maonekedwe ake akugwa. Chikuonetsanso [ndipo mofunika kwambiri] mpingo ukubwezeretsedwa ku malo ake a pachiyambi kuno ku nthawi yotsiriza.

Mpingo wapachiyambi sunagwe kuchokera ku bukhu la Chivumbulutso, chifukwa sunali gawo la malangizo wolembedwa kwa mpingo kuchiyambi. Ndi bukhu la mwala wapangodya, ndipo osati bukhu la maziko, ndipo kotero ndilongomasuliridwa kwa mpingo pano pa nthawi yotsiriza. Ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa mkwatibwi, ndipo Khristu akupanga chikondi ndi mkwatibwi wake pamene Iye akumupatsa iye mzimu wa vumbulutso ndi kuulura zinsinsi kwa iye. Ichi ndi chifukwa cha bukhuli, **"Bukhu [lomasuliridwa] la Chivumbulutso."** Ndi Mulungu kuika Chisomo Chachikulu [Machitidwe 4:33] pa mpingo wake mkwatulo usanachitike.

Komanso, mundirole ndilankhule, kuti owerenga ambiri a bukhu la Chivumbulutso alakwitsa potenga Yohane, mlembi, ngati Yohane nkonzi wa bukhu. Koma palibe njira iliyonse tinganene molondora kuti Yohane ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso. Iye anali mlembi, chotengera chabe chimene Mulungu anagwiritsa ntchito kufalitsa malingaliro Ake ku Mau olembedwa kuti awuluridwe pano mu nthawi yotsiriza. Yesu anali, ndipo ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso.

Momwemonso olemba bukhu ili akuzindikira mochuluka kuti NKONZI wa bukhu la Chivumbulutso ndi amene wapereka kudzoza kwa kumasulira kwenikweni kwa mlembi uyu. Kotero, ine ndikupemphera kuti mwapemphero inu mutenga kumasulira kwa bukhu la Chivumbulutso chifukwa mkwatibwi wa Khristu adzamvetsa bwinobwino zimene zikuchitika pano mu nthawi yotsiriza, chifukwa kuwala kwake [kumvetsa] ndi kowala ngati krustalo. [Chivumbulutso 21:11]

Komanso, ndiloreni ndinene ine -Ben Howard- kuti: kwa zaka zoposa 45 ndakhala ndikutumikira pa zolembedwa zimene zili mu bukhu ili, ngati mishonare mu maiko ambiri ndi kuno ku USA, mu mipingo, maholo, madera, nyumba zobwereketsa, ngati mlaliki wa pa wailesi, kufunsidwa mafunso, ndipo tsopano pa Internet, ngati m'busa wa **Sound of Liberty Assembly** moyandikana ndi Dawsonville, Georgia [USA] ndi mitundu ina ya malo wopezekamo anthu. Mwambiri mwa malo olankhulawa, kufunsidwa mafunso ndi zina, panali kujambulidwa matepi komanso kutenga mfundo zolemba pa zimene zimalankhulidwa zimene ine tsopano sindingathenso kuzilamulira.

- Kotero, zidziwike kwa onse: Kuti bukhu ili lapambana, ndipo laposa, zolembedwa zonse, zojambulidwa kapena mitundu ya nkhani zonse zotengedwa kuchokera kwa mlembi zimene zikuoneka ngati- kapena- zikutsutsana ndi zolembedwa izi, ngati zimenezo zinatengedwa mbuyomu lisanasindikizidwe bukhuli.
- Ichi ine ndikunena, chifukwa maulaliki ambiri pa matepi, ma CD, ma DVD, ma Video, komanso pa Internet apita ku madera ambiri padziko lonse kwa zaka zambiri zimene muli zochepa, ndipo mauthenga ena akale akhoza ngakhale kutsutsa zolemba izi, ine ndachita monga 2 Petro 3:18 amatiphunzitsa ife kuti *"Kukula mu chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye wathu."*

- Kotero, ine ndinena kwa inu kuti ine ndakhala mu utumiki uwu kwa zaka zambiri, monganso inu amene mukuwerenga ichi kwa nthawi yoyamba, kuti bukhu ili lidzapereka kuwala kwakukulu ku “Bukhu la Chivumbulutso” kusiyana ndi mauthenga anga akale amene inu mukhoza kukhala nawo, kaya pa tepi, kulembedwa mwa bukhu, kapena zolemba zanuzanu pa zimene mlembi anapereka, kaya zaka 45 zapitazo kaya zaka 5 zapitazo.
- Ichi ndikunena, chifukwa mzimu womwewo wa Chivumbulutso umene unamupangitsa Yohane kulemba Bukhu la Chivumbulutso wapangitsa kuti limasuliridwe pano mu nthawi yotsiriza kwa Mkwatibwi Wake.

Izi ndikulankhula mokhudzana ndi bukhu lonse la Chivumbulutso, ndipo silinapangidwe pa cholinga chochotsapo vumbulutso lililonse limene Mulungu akanapereka patsogolo kwa ine kapena wina aliyense wa atumiki woona wa Mulungu pa Bukhu la Chivumbulutso. Inu mukhoza kukhala otsimikizika kuti vumbulutso lenileni silidzatsutsana ndi zolemba izi.

Posachedwa, utumiki onse woona udzaoneka diso kwa diso [1 Akorinto 1:10] pa kumasulira uku pamene liwu la vumbulutso la Mulungu liyamba kulankhula kuchokera kumwamba mu kufotokoza kwakukulu mwa Mzimu Wake [Chivumbulutso 10:8] pa zinthu zimene mukufuna muwerenge.

Ndikupempheni inu owerenga, kuti muzindikire kuti zolembedwa izi ndi za okhawo amene ali ndi makutu auzimu kuti amve chimene Khristu akunena kwa mkwatibwi wake pamene Iye akupanga chikondi ndi iye, chifukwa Bukhu la Chivumbulutso ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa Mkwatibwi.

Kotero, mukatha kuwerenga bukhu ili, ngati silingadzutse wamkati wanu ndi kuwalira moyo wanu, ndiye pepani potenga nthawi yanu, ndipo chonde perekani bukhu ili kwa wina aliyense chifukwa chowaganizira mwa pemphero, mwina ndi lawo. Ine ndikukuthokozani mokoma chifukwa cha nthawi yanu ndi mgwirizano.

Pemphero langa kwa inu owerenga ndi ili: *Mulungu akupatseni inu mzimu wa nzeru ndi chidziwitso, ndi kuti maso akumvetsa kwanu awunikiridwe. Kuti mukamvetse masamba otsatira a bukhu ili. Bukhu ili likuthandizeni kuti muvale chovala choyera [Chivumbulutso 19:7-9], kuti musandulike mkazi wa Khristu pokhala m’modzi ndi Mau Ake munthawi yotsiriza iyi. Amen.*

Kuthokoza Kwapadera Kwa …

Ine ndikufunanso ndiwonetsere kuyamikira kwanga pa
ntchito
ya malemu William M.Branham mneneri wa Mulungu
wam'thenga
wa m'badwo uno wa Laodikaya komanso malemu mtumwi
Raymond M. Jackson
amene Mulungu anamugwiritsa ntchito kuti apitirize ntchito Yake imene Iye anaiyamba kupyolera mwa William Branham; makamaka mu gawo la mbiri la bukhu ili. Ngakhale ife sitili othandizidwa, kapena kukwezedwa ndi otsatira a
aliyense
wa uthenga wa amuna amenewa; zolemba zawo zinali zothandiza kwambiri pokonza bukhu ili.

Komanso, kuthokoza kwa padera kwa
Joyce Howard,
Gary Gentry,
Wanda Robertson,
Barbara Howard,
Leah Farruggia
ndi Enoch Kamanula
chifukwa cha kuthandiza mosatopa pa ntchito iyi.

"Ndipo anadza m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri, Nalankhula ndi ine, nanena, Idza kuno, ndidzakuonetsera iwe…" Chivumbulutso 17:1.

Lemba la pamwambali likuonetsa m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri amene akulankhulidwa kudutsa mu bukhu lonse la Chivumbulutso. M'modzi wa iwo akumuonetsa Yohane, amene akuimirira utumiki ngakhalenso kuimirira mkwatibwi, bukhu la Chivumbulutso. Kuona angelo asanu ndi awiri ndi kumvetsa ntchito zawo zimene iwo amachita ndi zinthu zopindula ku kumvetsa kwanu ku bukhu la Chivumbulutso. Izi zatsimikizidwa mu bukhu lonseli ngati chifungulo chenicheni chotsekula zinsinsi za [zoyamba] bukhu lozwizwitsa la Chivumbulutso.
.

MALONJE KU CHAPUTALA CHILICHONSE

Chaputala cha Chisanu ndi chinai

Chaputala chachisanu ndi chinai ndi kuomba kwa lipenga lachisanu ndi lachisanu ndi chimodzi. Pa kuomba kwa lipenga la chisanu dzenje lopanda malekezero likutsegulidwa ndipo ziwanda zikumasulidwa kuti zizunze mtundu wa anthu kwa kanthawi. **Ili ndi tsoka loyamba.** Pa kuomba kwa lipenga lachisanu ndi chimodzi, ziwanda izi zikusandulika ziwanda za nkhondo kutenga Kum'mawa Kutali ndi mafuko ena mu chimodzi kukonzekera nkhondo ya Armagedoni. Lipenga lotsiriza likulira pakati pa sabata. La chisanu ndi chimodzi likulira patsogolo pake mu gawo lotsiriza la sabata.

Chaputala cha Khumi

Chaputala cha khumi chikuonetsera chimene chikuchitika chisindikizo chachisanu ndi chiwiri chitatsegulidwa kumwamba mu 1963. Khristu akubwera ku dziko mu maonekedwe a m'ngelo kuti atenge iye mwini ulamuliro wofikitsa Mkwatibwi Wake ku umgwiro, **monga angelo asanu ndi awiri auzimu womwewo** amene anali ndi mibado yampingo isanu ndi iwiri ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri kuomba mau awo kupyolera mwa wamthenga wa mpingo wa m'bado wa chisanu ndi chiwiri.

Pa nthawi iyi, m'bado wa mpingo wa chisanu ndi chiwiri watha tchito monga yachitira mibado ina ya mpingo, ndipo Mulungu akuyamba kuchita ndi Mkwatibwi pamene zisindikizo zisanu ndi ziwiri zikutsegulidwa, ndipo bukhu lofunyulura likutsegulidwa mu dzanja la manja la Khristu. Khristu kenako akubangula ngati mkango. **Izi zikutipanga ife kudziwa kuti Iye ali pa dziko lapansi** mu maonekedwe awa, ndipo mosakhalitsa angelo asanu ndi awiri, amene anaikidwa kuthandiza Khristu mu mibado ya mpingo, akutsatira chitsanzo cha Khristu ndi kuomba ma liu awo onse palimodzi kuti atsirize "chinsinsi cha Mulungu," chimene chikuonetsera mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, imene ikulankhulidwa ku chaputala cha 13 cha Mateyu, ngati ufumu wa kumwamba. Pamene Yohane anamva mabingu akulankhula mu 96 A.D., iye anali pafupi kulemba chimene angelo analankhula, koma Mulungu analankhula kuchokera kumwamba kwa Yohane ndikuti usalembe. Mulungu anagwiritsa ntchito William Branham kutsegula mau kwa ife pamene zisindikizo zinatseguka kumwamba, Khristu asanabwere ku dziko ndi angelo asanu ndi awiri amene analankhula mawu awo kwa Yohane, ndipo zinauluridwa kwa M'bale Branham zimene zinanenedwa zimene Yohane sakanatha kulemba.

Vesi lachisanu ndi chiwiri la chaputala cha khumi likutidziwitsa kuti panthawi ya mabingu asanu ndi awiri wanthenga wapansi akutsiriza uthenga wake, chifukwa Chivumbulutso 10:7 tikuwerenga, *"Komatu m'masiku a mau a mngelo wa chisanu ndi chiwiri m'mene iye adzayamba kuomba, pamenepo padzatsirizika chinsinsi cha Mulungu, monga analalikira kwa akapolo ake aneneri."* Izi zikutionetsera ife kuti wanthenga wa chisanu ndi chiwiri akutsiriza uthenga wake pamene angelo asanu ndi awiri awa akuomba mau awo **<u>kupyolera mum au ake.</u>** [William Branham] kuulura zisindikizo zisanu ndi ziwiri kwa Mkwatibwi wa Khristu.

Vesi 8-10, ikutionetsera kuti chimene chili mu bukhu laling'ono si chimene mpingo wa zolowera, chifukwa ngakhale chikumveka bwino monga chikulalikidwira, **ndicholemererako**

kuchidya. Vesi 11 likutidziwitsa kuti ichi ndi chinthu cha dziko lonse ndipo chikuchitika pano. Ndi kulalikira kwa uneneri mwa utumiki usanu.

Chaputala cha Khumi ndi chimodzi

Chaputala cha khumi ndi chimodzi chikuonetsera kachisi kumangidwanso kumayambiriro kwa sabata la 70 la Danieli, pamene aneneri awiri okhala ndi mzimu wa Mose ndi Eliya pa iwo akunenera ku Israeli. Otsutsakhristu akuphwanya pangano pakati pa sabata ndi kupha aneneri awiri. **Ili ndi tsoka lachiwiri.** Chaputala ichi chikufotokozanso za lipenga lachisanu ndi chiwiri.

Chaputala cha Khumi ndi chiwiri

Chaputala cha khumi ndi chiwiri chikuonetsera mkazi wovala dzuwa, ndi mwezi kumapazi ake, ndi korona wa nyenyezi khumi ndi ziwiri pa mutu wake. Mkazi uyu ali ndi mwana ndipo wabeleka mwana wa mwamuna. **Uyu ndi Israeli pamene iye wabereka Khristu.**

Chaputala ichi chikuonetseranso chinjoka chofiira chachikulu chokhala ndi mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi. **Uwu ndi ufumu wa Chiroma** kudutsa mu nthawi pamene ukufotokoza za kubwera koyamba kwa Khristu komanso kuno mu nthawi yotsiriza. Aroma anayesera kumupha Yesu ali mwana. Kenako itatha ntchito Yake, Iye anapachikidwa pa mtanda ndi kupita ku mpando wa chifumu wa Mulungu. Mkazi yemweyu amene adabereka mwana wa mwamuna akuoneka apa, pafupifupi zaka 2000 zitatha akuthawa pa maso pa chinjoka kupita mu chipululu ku malo amene Mulungu amukonzera iye kuthawa pamaso pa asirikari a papa mu nthawi ya zaka zitatu ndi theka zotsiriza za sabata la 70 la Danieli. Chaputala ichi chikuonetseranso satana akuponyedwa kuchokera ku mwamba, **chimene ndi tsoka lachitatu.**

Chaputala cha Khumi ndi chitatu

Chaputala cha khumi ndi chitatu chikuonetsera zirombo ziwiri, choyamba chimene chikutuluka nyanja ndi chinjoka cha Chivumbulutso 12. Ndi Ufumu wa Chiroma kubwezeretsedwa kwathunthu ndi chirombo chachiwiri chokhala ngati mwana wa nkhosa wa chaputala 13. **Chirombo chokhala ngati mwana wa nkhosa ndi mwantheradi U.S.A.** Fano la chirombo ndi Bungwe la Mipingo Padzikolonse. Limene linali ndi chiyambi chake ku U.S.A. Chaputala ichi chikuonetsera chilemba cha chirombo, komanso **nambala 666.**

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHACHISANU NDI CHINAI

Atatha kuomba malipenga anai mu chaputala 8, mngelo akuuluka ndipo akunena, *"Tsoka, tsoka, tsoka, kwa onse okhala pa dziko."* Zimenezo zikutibweretsa ife ku chaputala chachisanu

ndi chinai, chimene chikufotokoza malipenga awiri, chachisanu ndi chachisanu ndi chimodzi. Lipenga lachisanu likuomba pakati pa sabata. Iyi ndi nthawi imene papa akuphwanya pangano ndipo aneneri awiri akuphedwa.

Musaphonye nthawi iyi. Izi ndi pakati pa sabata. Machenjezo onse a Mulungu akanidwa ndipo iye akutsegula phompho ndi kulora ziwanda kutuluka kubwera pa dziko chimene ndi tsoka loyamba.

Vesi 1: *"Ndipo mngelo wachisanu anaomba, ndipo ndinaona nyenyezi yochokera kumwamba idagwa pa dziko; ndipo anampatsa iye chifunguliro cha dzenje la phompho."*

Vesi 2: *"Ndipo anatsegula pa dzenje la phompho; ndipo unakwera utsi wotuluka m'dzenjemo, ngati utsi wa ng'anjo yaikulu, ndipo dzuwa ndi thambo zinada, chifukwa cha utsiwo wa kudzenje."*

Palibe amene adzaona nyenyezi ikugwa kuchokera kumwamba. Phompho likuimirira kukhalapo kwa satana, kumene ziwanda zikusungidwa mpakana Mulungu atakonzeka kuzimasura. Inu ngati mukanakhala mudzenje pa mtima wa dziko, inu mukanangopita, pakanakhala popanda pothera pa ilo. Chifukwa pamene inu mufika pamwamba pa dziko, pakanakhala potseguka. Limenelo ndiye dzenje lopanda pothera.

Imeneyo idzakhala nthawi ya m'dima pakati pa sabata. Pamene phompho litsegulidwa, ndipo zanenedwa kwa satana, m'dierekezi, "Iwo anandikana ine. Iwo akana Mau. Pitani kunja uko." Mugawo lauzimu Yohane anaziona izo ngati winawake amene anabwera ndi kutsegula dzenje. Palibe malo ena aliwonse pa dziko kumene kuli dzenje ndi chovindikira pa ilo limene lili ndi ziwanda zonse kutsekeredwa mu ilo. Yohane amayenera kuziona mu njira iyi kuti zikalembedwe kuti tikathe kuziona kuchokera ku izo mwa kumasulira kwa Mulungu. Izi zonse ndi chinthu cha uzimu. Kweni kweni, mu njira zambiri mdierekezi akuyamba mochuluka ndi mochuluka kukhala ndi ulamuliro mu dziko lero. Yohane anaona ichi ngati mngelo amene anabwera nditsegula dzenje ndipo utsi wakuda waukulu unatuluka. Utsi unali wakuda kwambiri moti unaphimba dzuwa. Kenako, kuchokera mu utsi munayamba kutuluka dzombe. Musaiwale, kuti awa ndi masophenya; ndi zauzimu.

Vesi 3: *"Ndipo m'utsimo mudatuluka dzombe pa dziko, ndipo analipatsa ilo mphamvu monga zinkhanira za dziko zili ndi mphamvu."*

Ziwanda zomwezi zimene zili pansi pa lipenga la chisanu ndi zomwezi zimene zili pansi pa lipenga lachisanu ndi chimodzi. Koma pansi pa lipenga lachisanu iwo apatsidwa mphamvu monga zinkhanira. Chinkhanira chimaluma mopweteka, koma nthawi zambiri sizimangitsa kupweteka koopsa. Zimangokupangani inu kukhala ankhawa. Ndi chinachake chosautsa ndi kuzunza mtundu wa anthu.

Pansi pa lipenga lachisanu iwo sadzapha aliyense, koma adzangozunza ndikupanga mtundu wa anthu kukhala wa nkhawa pamene Mulungu akuwalora iwo. Ichi ndicho cholinga cha ziwanda izi; chifukwa dziko la pansi lakana chenjezo cha Mulungu. Kotero Mulungu akulora phompho kuti litsegulidwe ndipo akunena, "Apo iwo ali, adierekezi; pitirizani. Musawaphe iwo, koma tangowazunzani iwo. Iwo andikana ine. Iwo akana Mau. Iwo akana chifundo, kotero tangowazunzani." Ndi chimene Mulungu akunena kwa ziwanda izi.Yohane anaziona ngati kutsegulidwa kwa phompho ndi kulora utsi kutuluka mu ilo.

Vesi 4: *"Ndipo ananena kwa ilo kuti lisaipse udzu wa pa dziko, kapena chabiriwiri chili chonse, kapena mtengo uli wonse, koma anthu amene alibe chizindikiro cha Mulungu pa mphumi pawo ndiwo."*

Vesi 5: *"Ndipo anapatsa ilo mphamvu sikuti likawaphe, komatu kuti likawazunze miyezi isanu; ndipo mazunzidwe awo anali ngati mazunzudwe a chinkhanira, pamene chiluma munthu."*

Ku m'mawa chapakati pali nthawi zimene kumakhala miliri ya dzombe ndipo limatha kudya zomera, thengo ndi zina zotero. Ndi m'mene ziwanda izi zidzachitira anthu mu nthawi imeneyo. **Zidzawadyera zonse zakulingalira kwa mzeru zawo.** Zidzawadyera chilichonse chanzeru ndi cha umulungu ndipo iwo adzangokhala zolengedwa zankhawa.

Ife timalankhula za zopanda pake zimene zikuchitika lero, koma sitinaonepo chili chonse. Ndi ziwanda zimene zikungojowajowa pang'ono, koma limodzi la masiku awa Mulungu adzati "ziwanda, apo ali," ndipo anthu adzakhala ngati zomera zimenezo za kum'mawa chapakati m'mene amakhalira ndi miliri ya dzombe. Ziwanda zidzawakwawira monse ndi kumadya chilichonse chimene ali nacho. Idzakhala nthawi ya nkhawa. **Inu mukukamba za hade pa dziko, ndi m'mene zidzakhalire pamene ziwanda izi zimasulidwa kumtundu wa anthu.**

Tayang'anani, iwo sadzaononga zinthu zobiriwira. Chimenecho chikutiuza chiyani ife? Izo zikutiuza kuti sidzombe la chilengedwe, chifukwa dzombe la chilengedwe limadya masamba a mitengo ndi zina zotero. Izi zikutionetsera ziwanda zauzimu zimene zatumizidwa kudzazunza iwo amene akana Mau a Mulungu. Iwo sangathe kuononga iwo amene ali ndi chisindikizo cha Mulungu.

Mau oti *"kuzunza (idwa)"* ali mu vesi lachisanu, nthawi zitatu. Kodi mukuona chimene ziwanda izi ziri, tsopano? Izo ndi zoti zizunze mtundu wa anthu. Pali nthawi yapadera imene Mulungu akuti awazunze iwo *mwa kanyengo ka nthawi*, koma osawapha iwo. Zinkhanira za uzimu izi zikungowaluma iwo mu uzimu. Anthu sangathe kuzimverera izo ndi matupi awo athupi, koma nthawi zina adzafuula ndikuchotsa tsitsi lawo. Ndi ziwanda kuwazunza iwo. Ife tangoona pang'ono za izo, chifukwa Mulungu akuzigwira, koma iwo akungojowajowa.

Kuli ziwanda lero. Anthu ambiri ndiwodzazidwa ndi ziwanda. Anthu ambiri akuzunzidwa ku imfa lero. Inu mukhoza kuwafunsa, "chavuta ndi chiyani?" Ndipo iwo adzati, "Ine sindikudziwa," koma ichi ndi chinthu chaching'ono ku chimene chidzakhale pamene chovindikira cha ku phompho chidzachotsedwa.

Vesi 6: *"Ndipo m'masiku ajawo, anthu adzafunafuna imfa osaipeza konse; ndipo adzakhumba kumwalira, koma imfa idzawathawa."*

Ine ndinamva mlaliki wa chipentekosite akunena nthawi ina kuti kudzakhala tsiku limene simudzafa. Iye anati ngati mutamudula munthu mutu, iye adzakhalabe ndi moyo; kapena mudzamuombera ndikudzazidwa ndi mabowo koma iye adzapitirirabe kukhala ndi moyo. Iye anati kuti Baibulo linati kuti iwo adzafunafuna imfa ndipo imfa idzathawa, ndipo imfa idzasowa ndipo iwo sadzafa. Iye amangolima m'malo molalikira. Izi sizikutanthauza chimenecho konse. Izi zikuonetsa kuti ziwanda izi sizinaperekedwere kupha. Anthu ambiri adzazunzidwa mu nthawi imeneyo, ndipo iwo adzati kunali bwino kufa, ndipo adzafuna Mulungu atawalora iwo kufa. Kudzakhala kugwirira, kupha, ndi chisawawa pa dziko lonse lapansi. **Adzakhala mwamtheradi hade padziko ndipo anthu adzati zikanakhala bwino osabadwa kusiyana ndi kukhala ndi moyo muchivundi ichi.** Ziwanda izi sizinaperekedwe kuti ziphe anthu.

Inde, padzakhala akupha mu nthawi imeneyo, koma ntchito yoyamba ya ziwanda izi sidzakhala kupha wina aliyense; idzakhala kuzunza iwo ndi kuwapanga iwo ankhawa.

Vesi 7: *"Ndipo maonekedwe adzombelo anafanana ndi akavalo okonzeka kukachita nkhondo; ndi pa mitu pao ngati korona onga agolide, ndi pankhope pao ngati pa nkhope anthu."*

Izi zikunena kuti maonekedwe adzombelo amaoneka ngati akavalo okonzekera nkhondo. Izi zikubwera patsogolo pake pamene zikusandulika ziwanda za nkhondo, pamene tibwera patsogolo mu chaputala ichi pansi pa lipenga lachisanu ndi chimodzi.

Vesi 8: *"Ndipo anali nalo tsitsi longa tsitsi la akazi, ndipo mano ao anali ngati mano amikango."*

Vesi ili la chisanu ndi chitatu likuonetsera poyera chithunzi chimene mukuchiona pamene muyang'ana m'miseu lero ndikuona anyamata okhala ndi tsitsi lalitali. Atsikana ang'ononso akudzigulitsa okha kwa m'dierekezi, koma tsitsi lalitali la anyamata likuonetsaera kuukira.

Chimene tikuchiona lero ndi chabe choonetsera mtsogolo. Chinthu chenicheni sichifika mpakana aneneri awiri ataphedwa pakati pa sabata. Kodi mukutha kuona chifukwa chake Baibulo likuti, padzakhala nthawi ya mavuto ndipo idzafara mpaka itafika pa dziko lonse.

Kodi mungathe kugwira pang'ono mwa mzeru za m'mene kudzakhalire pamene chifundo cha Mulungu chidzachotsedwa pa dziko lino ndipo Iye adzamasula adierekezi? Mwa uzimu inu mukhoza kuganiza kuti munali ndi nthawi yovuta ndi kukhala ankhawa. Inu mukhoza kuganiza kuti munali osautsika mu nzeru, koma inu muli padzuwa pa phwando mukazifanizira ndi izi. Yembekezani mpakana ziwanda izi zimasulidwe. Akhristu ndi onse amamverera chipsinjo cha tsiku limene tikukhala, koma pakali pano Mzimu Woyera wagwira mphamvu iyi. Koma Mulungu adzati, "Tsegulirani dzenje, tsegulani chovindikira, ndipo ziloreni ziwanda zituluke." Akuti izo zinalinso ndi mano ngati mikango, ilo ndi gawo la nkhondo pansi pa lipenga lachisanu ndi chimodzi.

Vesi 9: *"Ndipo anali nazo zikopa ngati zikopa zachitsulo; ndipo mkokomo wa mapiko awo ngati mkokomo wa agaleta akavalo ambiri akuthamangira kunkhondo"* [Izi zikuonetsera kuti iwo akukonzekera zochita zina pa lipenga lachisanu ndi chiwiri.]

Vesi 10: *"Ndipo ziri nayo michira yofanana ndi ya chinkhanira ndi mbola; ndipo m'michira mwao muli mphamvu yao yakuipsa anthu miyezi isanu."*

Kodi munali chiyani m'michira? Mbola ya chinkhanira. Ine ndikufuna kuti mugwire zimenezo chifukwa pansi pa lipenga lachisanu ndi chimodzi pali michira yokhala ngati maserpenti, ndipo ili ndi mitu, ndipo ndi izo imaluma, imapha. Pansi palipenga lachisanu sizinapatsidwe kwa iwo kupha, koma kuvulaza. **Ndipo mbola ya chinkhanira imeneyo ndi mbola yauzimu ku moyo wa mtundu wa anthu amene adzakhala pano padziko mkwatulo utachitika.** Kumbukirani kuti iwo sioti aphe, koma kuvuraza.Motani? Mwauzimu. Ndipo padzakhala kuvuraza kwa uzimu mu nthawi ino, koma ntchito yoyamba ya ziwanda izi sikupha.Yohane akuzipanga momveka kuti ndi kuzunza anthu, kuwapanga iwo ankhawa, kuwavulaza iwo, koma osawapha. Pali mphamvu yochepa kwambiri yozunzira kwa iwo. Mulungu akuti osawapha iwo, koma kuwapanga iwo ankhawa ndikuwavuraza iwo.

Vesi 11: *"Ndipo linali nayo mfumu yakuilamulira, mngelo wa phompho; dzina lache mu chihebri Abadoni, ndi mu chihelene ali nalo dzina Apoliyoni."*

Dzina la mngelo ameneyo likuonetsa kugwira ntchito kwa ziwanda izi. "Apoliyoni" akutanthauza *kuononga.* Inu mukhoza kuganiza kuti muli ndi nyumba yotetezedwa, koma padzakhala anthu amene adzakhala akungoyendayenda m'makwalala, ndipo cholinga chawo chokhacho ndi kuononga, kupanga nkhawa, ndi kuzunza anthu. Satana adzagwiritsa mtundu wa anthu akugwa ndi achinyamata a lero amene adzigulitsa okha kwa mdierekezi. Inu simudzakhala otetezeka mu chipinda chanu chochezera kuonera television, chifukwa iwo adzakhala akuthyola. Ndi chimene dzinalo likutanthauza, kuononga.

Vesi 12: *"Tsoka loyamba lapita; taonani, akudzanso matsoka awiri mtsogolomo."*

Pali atatu amatsoka amenewa. Matsoka atatu amenewa akuchitika mu miyezi chabe pakatikati pa sabata ndi kuomba kwa lipenga lachisanu.

Vesi 13: *"Ndipo mngelo wachisanu ndi chimodzi anomba, ndipo ndinamva mau ochokera ku nyanga za guwa la msembe lagolide liri pamaso pa Mulungu."*

Vesi 14: *"Nenana kwa mngelo wa chisanu ndi chimodzi wakukhala ndi lipenga, masula angelo anai omangidwa pa mtsinje waukuru Firate."*

Vesi 15: *"Ndipo anamasula angelo anai, okonzeka kufikira ora ndi tsiku ndi mwezi ndi chaka, kuti akaphe limodzi la magawo atatu a anthu."*

Pansi pa lipenga la chisanu ziwanda izi sizoti ziphe, koma apa ziwanda zomwezi zikuuzidwa kupha anthu, kupha gawo la chitatu la anthu.

Chimene tikuona pamene mngelo wachisanu ndi chimodzi aomba si angelo anai omangidwa ndi maunyolo, koma ndi angelo anai okhala ndi ulamuliro woletsa mphamvu, kuti asabweretse dziko ku Armagedoni kufikira akapolo a Mulungu asindikizidwe. **Apa, 144,000 asindikizidwa, aneneri awiri aphedwa, ndipo Mulungu akutsegula hade pa dziko.**

Pa nthawi iyi, Mulungu akutsegula mphepo zinai: mphepo za chipembedzo, mphepo za nkhondo, mphepo za chuma, ndi mphepo za ndale. Lipenga la chisanu ndi chimodzi ili likupanga kachitidwe kamene mlili wachisanu ndi chimodzi wa pa Chivumbulutso 16 umalankhula za iwo, kumene akuti mizimu itatu yodetsedwa yonga achule inatuluka mkamwa mwa chinjoka, chirombo, ndi mneneri wabodza- kuonetsera m'mene ziwanda izi zinapita mu magawo osiyanasiyana a wanthu kubweretsa dziko ku Armagedoni ku mapeto asabata.

Mulungu akuuza ziwanda kuti zizunze anthu mpakana Iye atakhutitsidwa ndi izo, ndipo kuti zipite ndikukhala ziwanda zachisirikali kuti abweretse dziko la pansi ku Armagedoni. Nthawi iyi Iye akuziuza izo kuti osati kuzunza kokha koma kuwapha iwo, kupha pafupifupi gawo lachitatu. Pamene Armagedoni achitika, akuti mwazi udzakhala ukuyenda mwa akavalo. Sizikutanthauza kwenikweni kuti akavalo adzakhalapo, koma kuti padzakhetsedwa mwazi wambiri.

Vesi 16: *"Ndipo chiwerengero cha nkhondo za apakavalo ndicho zikwi makumi awiri zochulukitsa zikwi khumi; ndinamva chiwerengero chawo."*

Vesi 17: *"Ndipo kotero ndinaona akavalo m'masomphenya, ndi iwo akuwakwera akukhala nazo zikopa za moto, huakinto ndi sulfure; ndi mitu ya akavalo ngati mitu ya mikango, ndipo mkamwa mwao munatuluka moto ndi utsi ndi sulfure."* [Izi ndi ziwanda zomwezo pansi pa lipenga lachisanu, koma zikungogwira ntchito yosiyana.]

Vesi 18: *"Ndi miliri iyi linaphedwa limodzi la magawo atatu a anthu, ndi moto, ndi utsi ndi sulfure, zotuluka mkamwa mwao."*

Kodi mukuona kusiyana kwake? Pansi pa lipenga lachisanu iwo anali oti asaphe, koma pansi palipenga lachisanu ndi chimodzi iwo ndiwoti aphe. Lipenga lachisanu linali lozunza anthu, koma pansi pa lipenga lachisanu ndi chimodzi iwo akubweretsa dziko la pansi ku Armagedoni kuti aphe. Kudzakhala kupha, ndipo anthu mamiliyoni mazana awiri adzafa ku malo oyera mu nkhondo ya Armagedoni. Ziwanda izi zikupita kuwasonkhanitsa iwo. Kumbukirani kuti awa ndi masomphenya, koma mu zenizeni padzakhala mavuto akulu mu Dziko Loyera.

Vesi 19: *"Pakuti mphamvu ya akavalo ili mkamwa mwao, ndi m'michira yawo, pakuti michira yawo ifanana ndi njoka, nikhala nayo mitu, ndipo aipsa nayoyo"*

Ziwanda zomwezo mu lipenga lachisanu zimafanana ndi zinkhanira zokhala ndi mbola, ndipo zinali zoti zizunze. Apa, m'malo mokhala ndi mbola za zinkhanira ku michira yawo, ziri nayo mitu ya serpenti ndipo akuluma nayo kuti aphe ndi kuononga. Ndi kusintha kwa zinthu; ndipo mkwiyo wa Mulungu ndi chiweruzo zikuyamba kutsanuridwa mu muyeso waukulu. **Iye akuyamba kulibweretsa dziko lapansi mu maonekedwe a Nkhondo ya Armagedoni.** Inu mukakamba zakupha ndi kuphana, ziwanda izi ndi zakuti ziphe gawo lachitatu la anthu pa dziko. Ziwanda zomwezo zimene zinauzidwa kuzunza zikuuzidwa tsopano kuti zipite kukapha.

Kodi inu mungakonde kulumidwa ndi chinkhanira kapena kulumidwa ndi serpenti ya chiphe? Awa anali masomphenya. Yohane anaona akavalo, okhala ndi mchira ngati njoka yaikulu imene

imayenera kuluma ndikupha anthu. **Awa anali masomphenya, koma kumasulira kwake ndi uku: ndi ziwanda. Poyambirira zimayamba ngati chipsinjo monga chimene chikubwerera pa dziko lapansi lero, chipsinjo cha ziwanda, zimphamvu, zimene zimangopanga moyo kutuluka mpakana potsiriza akunena kuti kunali bwino kufa kusiyana ndi kukhala ndi moyo,** koma lipenga ili lachisanu ndi chimodzi likuomba ndipo iwo akuyamba kupha ndi kubweretsa anthu kunkhondo ya Armagedoni.

Vesi 20: *"Ndipo otsala a anthu osaphedwa nayo miliri iyo sanalapa ntchito ya manja awo, kuti asapembedzere ziwanda ndi mafano agolide, ndi asiliva, ndi amkuwa, ndi amwala, ndi amtengo, amene sakhoza kupenya, kapena kumva, kapena kuyenda."*

Vesi 21: *"Ndipo sanalapa mbanda zao, kapena nyanga zao, kapena chigololo chao, kapena umbala wao."*

Tayang'anani kuti akuti "akupha," ambiri. Idzakhala nthawi ya kupha ndipo palibe amene adzakhala otetezeka mu nyumba ili yonse. Inu mukuyenera kudzakhala ndi asilikari kuyang'anira nyumba yanu kuti mukhale otetezeka mu nthawi imeneyo.

Vesi lotsiriza ili likuonetsera kutha kwa chikhalidwe, ndipo tikuziona lero dama, ndi zina zotero. Izo zikupitiriranso mu dama la uzimu.

Iwo sanalape. Chifukwa chiyani? Mulungu amayenera kukuitanani inu musanalape. Iye anati palibe munthu adzabwera kwa ine pokhapokha Mzimu utamuitana iye. **Mulungu amachotsa Mzimu Wake palibe kulapanso pamenepo.** Palibenso kulapa lero kumene kwatsala. Zidzakhala motani pamene chifundo cha Mulungu chichoka kwathunthu? Palibe kulapa. Iwo sadzalapa pa kupembedza mafano agolide ndi siliva kapena dama lawo ndi kupha kwao. Iwo anali okondwa anachita izo, chifukwa icho ndi chikhalidwe chao. Icho ndi chikhalidwe cha m'dierekezi, koma ife tikufuna chikhalidwe cha Khristu. Ameni.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA KHUMI

Chaputala cha khumi cha Bukhu la Chivumbulutso ndi zochitika zimene zikuyamba kuchitika nthawi yomweyo Mwana wa nkhosa atatha kumasula chisindikizo cha chisanu ndi chiwiri, ndi kubwera ku dziko ngati Mngelo Wamkulu. Powerenganso Chivumbulutso, chaputala chachisanu ndi chitatu, vesi loyamba- *"Ndipo pamene anamasula chisindikizo chachisanu ndichiwiri, munali chete mwamba monga mwa nthawi ya ora latheka."* Kumasula kwa chisindikizo chachisanu ndi chiwiri ichi chikutsiriza ntchito ina ya angelo asanu ndi awiri awa. Tsopano pamene iwo abwera pa dziko ndi Khristu, akulankhula mau awo kuulura zinsinsi zisanu ndi ziwiri zimene zatsegulidwa kale mbuyomu ku mwamba Khristu asanabwere kutsika kudziko. Angelo auzimu awa akulankhula mau awo kupyolera mu mau awanthenga wa ku mbado wa chisanu ndi chiwiri [William Marion Branham]. Uku ndi kulira kwa mabingu asanu ndi awiri amene Yohane anauzidwa kuti asalembe ndipo akutsiriza "chinsinsi cha Mulungu" mu Chivumbulutso, chaputala 10:7. Chinsinsi ichi ndi njra imene mpingo unatenga pamene unayamba kugwa kuchokera ku "chikondi choyamba" Izi zikuchitika **pokhapo** bukhu laling'ono limene linatsegulidwa kale kumwamba ndi kubweretsedwa ku dziko ndi Khristu, Mwiniyekha, monga Mngelo Wamkulu wapa Chivumbulutso, chaputala 10:1.

Ine ndikufuna kuchita ndi chaputala ichi mu njira yosiyana, kusiyana ndi machaputala ena, chifukwa cha maonekedwe azochitika zimene zalembedwa apa. Ine ndikufuna ndikupatseni kufotokoza kwa chinthunzi chonse ife tisanafike ku malemba. Kotero pamene tiwerenga

malemba zidzakhala zomveka zimene Yohane adaona, ndipo tikhoza kuona kuti ndi Khristu mu Mpingo Wake mu nthawi yotsiriza.

Monga taphunzira zisindikizo mu chaputala cha chisanu ndi chimodzi, ife taona bukhu lofunyulura lokhala ndi zomatira zisanu ndi ziwiri [kapena zisindikizo] mozungulira ilo. Bukhu lofunyulurari silikanatha kutsegulidwa pokhapokha ngati pakadali chomatira pa ilo. Zonse za zisindikizo zisanu ndi chimodzi zimene zinatsegulidwa mu chaputala chachisanu ndi chimodzi, zikuimirira, mwazina, nyengo ya nthawi. Chisindikizo chachisanu ndi chiwiri chikuimiriranso nyengo ya nthawi. Chikuimirira nyengo ya nthawi imene ikuonetseredwa ngati kukhala chete kumwamba; koma nyengo iyi siiri ya chete pa dziko, chifukwa ikuimirira mfundo ya kuti Yesu akubwera pa dziko mu maonekedwe amngelo zisindikizo zisanu ndi ziwiri zitatha kutsegulidwa ku mwamba. Izi zimapangitsa chimwemwe chachikulu pa dziko pakati pa Mkwatibwi, koma chete mwamba chifukwa mkazi wake wabwera kudzamutenga iye kukonzekera kupita mu Mkwatulo. Izi zonse zikuchitika chisautso chisanayambe kuchitika pa dziko. Komanso, ine ndikufuna kuika chidziwitso chapadera apa: **Mu chaputala ichi, tikuchita ndi mfundo yakuti Khristu wabwera pa dziko. Izi sikuti ndi mu maonekedwe a thupi. Munthu ameneyo, Khristu Yesu, akadali kukhala pa mpando wa chifumu wa Atate pamene chaputala ichi chikukwaniritsidwa. Monga m'mene Yesu anali mu mpingo wake mu maonekedwe auzimu mpingo usanagwe ku Mau, kotero Iye wabweranso mwa Mkwatibwi wake pamene iye akubwereranso ku vumbulutso lathunthu la Mau. Koma "Khristu mu thupi" akukhala pa mpando wa chifumu wa Mulungu mpakana mkwatulo wa Mkwatibwi wake, ndipo ulamuliro wonse umayambira pamenepo.**

Komanso, mu chaputala ichi pali <u>mitundu</u> itatu ya maliu <u>auzimu</u>, ndipo onsewa ndi omvera Mzimu Wamuyaya. Choyambirira pali liu la Mngelo Wamkulu [Khristu mu maonekedwe a mngelo] pamene Iye akubangula ngati mkango. Kenako pali maliu a [angelo auzimu] mabingu. Kachitatu, pali liu lochokera kumwamba, limene ndi liu la Mzimu Wamuyaya [Mulungu] limene likuomba kudzera mu thupi la Yesu Khristu limene likukhala pa mpando wachifumu wa Atate Wake pamene chaputala ichi chikukwaniritsidwa, ngakhale Khristu ali pano, koma mu maonekedwe a mngelo. Apa ndipamene ena mwa oyeramtima a Mulungu amaganiza kuti Khristu salinso pa mpando wa chifundo, pamene Mngelo Wankulu akubwera ku dziko kudzakwaniritsa chaputala ichi. Koma Khristu adakali pa "mpando wa chifundo" pamene chaputala ichi chikukwaniritsidwa.

Taonani, ndizofunikira kwambiri mu chaputala ichi kutenga kanthawi pang'ono kulingalira pa Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu imene ikulankhulidwa mu Chivumbulutso chaputala 1:4 ndi chimene iwo amasandulika kwa Mkwatibwi pamene iwo apatsidwa ntchito zawo zosiyanasiyana. **Pamene Yohane anaona angelo asanu ndi awiri kwa nthawi yoyamba, iye adawaona iwo ngati Mizimu isanu ndi iwiri yosakhala nayo ntchito ina ili yonse. Kotero analibe maonekedwe kupatula Umulungu, kuonetsera cha ntchito zimene akuchita.** Mwa chitsanzo, mizimu isanu ndi iwiri itasandulika angelo ku mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, iwo akuonetseredwa ngati nyali za moto zisanu ndi ziwiri kuyaka pa mpando wa chifumu. [Chivumbulutso 4:5] Zoikapo nyali zisanu ndi ziwiri zikuimirira mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Kotero, mu Chivumbulutso chaputala chachisanu, iwo akudziwika ndi nyanga zisanu ndi ziwiri ndi maso asanu ndi awiri pa Mwana wa nkhosa pamene Iye akutenga bukhu kutsegula zisindikizo zisanu ndi ziwiri. Kotero, mu chaputala ichi, angelo asanu ndi awiri omwewo akutchedwa **"mabingu."** Awa ndi angelo asanu ndi awiri amene akulankhulidwa kudutsa mu bukhu lonse la Chivumbulutso. Iyi ndi mfundo yofunika kwambiri pa kumvetsa Bukhu la Chivumbulutso. Izi zimatithandizanso kudziwa nthawi imene ife tikukhala podziwa ntchito

zosiyanasiyana zimene angelo awa amachita, ndi nthawi imene ntchito iliyonse ikuyenera kuchitika. Pamene mibado ikutha, zisindikizo **zikutsegulidwa kumwamba,** ndipo kulankhulidwa kwa mabingu asanu ndi awiri ndi "zinsinsi" zimene zikuyenera kuuluridwa kwa Mkwatibwi, kupyolera mwa wanthenga wa m'bado wachisanu ndi chiwiri. Zimenezo zatsirizika tsopano, pamene "mabingu" anaulura chimene chinachitika kumwamba pamene zisindikizo zinamasulidwa kumeneko. [Chivumbulutso, chaputala 10:7]

Chivumbulutso 5:5-7, chikutionetsera chithunzithunzi cha Mwana wa nkhosa, pamene Iye anatenga bukhu mu dzanja la manja la Iye amene akhala pa mpando wa chifumu. Apa ife tikuona kuti mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu yasandulika gawo la Mwana wa nkhosa pogwira ntchito yake mu dziko mu nthawi ya mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, ndiko kusandulika gawo la Mwana wa nkhosa ngati maso asanu ndi awiri komanso nyanga.

Taonani ichi, mpingo usanagwe ku Mau mu m'bado oyamba, Mwana wa nkhosa samaoneka ngati kuti ali nawo maso ndi nyanga zisanu ndi ziwiri. Iye amakhala nako kudziwika uku mu nthawi ya mibado ya mpingo pamene Iye anakhala pa udindo wa Wansembe Wankulu, ndi kumapereka msembe ya machimo a mpingo wake wakugwa. Pamene anali pa udindo wa Wansembe Wankulu, angelo asanu ndi awiri mokhulupirika anagwira ntchito yake padziko, pokhala gawo la Mwana wa nkhosa. Ichi chikutanthauza kuti aliyense amene akhala ndi vumbulutso loona la Mwana wa nkhosa wa Mulungu pano pa mu nthawi yotsiriza, ayenera kukhala ndi vumbulutso la ntchito zisanu ndi ziwiri za Mwana wa nkhosa kudutsa mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Inde, Khristu anagwira ntchito kupyolera mwa angelo asanu ndi awiri, kapena mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu kuulura Mau ku m'bado uliwonse kwa wanthenga nyenyezi imeneyo. Poti angelo asanu ndi awiri ali pansi pa ulamuliro wa Khristu ndipo iwo mokhulupirika anamumvera Iye, izi zinawapanga iwo kukwanira kubweranso padziko ndi Khristu. Mu chaputala cha khumi ichi cha Chivumbulutso, Khristu akubweretsa vumbulutso lathunthu la Iyemwini ku dziko ku ungwiro wotsiriza wa oyeramtima. M'bale Branham anati, "Mzimu Oyera unatumiza m'modzi mwa amithenga awa [angelo] usiku uliwonse pamene iye amalalikira zisindikizo zisanu ndi ziwiri." [Izi zinachitika mu 1963].

Zalengezedwa ndi Mngelo Wamkulu kuti "palibenso nthawi" ya Khristu kukhala ndi chifundo pa nansongole ndi tirigu kukulira limodzi. Nansongole tsopano walekanitsidwa ndi mkwatibwi wa Khristu, ndipo izi zikutanthauza kuti palibenso ntchito yopereka msembe ya mtundu umenewo kwa iwo; ngakhale kuti pali chifundo kwa mbewu ya Mulungu mu magawo ena a dongosolo lake la chiombolo. Ma liu a angelo asanu ndi awiri awa, kapena Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu akuomba mabingu palimodzi pakufikanso uku kudziko, kudzagwirizana ndi mau a Khristu, kudzatsiriza dongosolo la Mulungu la Mkwatibwi wa Khristu Mkwatulo usanachitike. Izi zimatsiriza chinsinsi cha Mngelo wamkulu chimene chikubangula ngati mkango ndi maliu amabingu asanu ndi awiri auzimu. Iwo akuoneka ngati gawo la Mwana wa nkhosa mu chaputala chachisanu cha Chivumbulutso. Iye amene akuonetseredwa ngati Mwana wa nkhosa wokhala ndi nyanga zisanu ndi ziwiri komanso maso asanu ndi awiri, ndi iye amene anatenga bukhu. Iye akuonetsedwa mu chaputala cha khumi padziko ngati Mngelo Wamkulu ali ndi bukhu lotsegula **zisindikizo zonse zitatsegulidwa kumwamba.** Vumbulusto la zisindikizo izi laperekedwa kwa wamthenga wa mpingo wa m'bado wachisanu ndi chiwiri, ndi angelo asanu ndi awiri amene anaomba. Angelo asanu ndi awiri awa analankhula mau awo kupyolera mwa wanthenga wa m'bado wa mpingo wa chisanu ndi chiwiri kuonetsera njira imene mpingo udadutsamo kudutsa mu nthawi, koma apa, [muchaputala chakhumi], onse asanu ndi awiri akulankhula kupyolera mwa wanthenga wa mpingo wa m'dado wachisanu ndi chiwiri kutsiriza "chinsinsi" cha Mulungu.

Mundilore ine ndibwerezenso kunena kuti angelo asanu ndi awiri awa kudutsa mu nthawi, anapereka Mau Mulungu kwa nyenyezi [wanthenga wapansi] munthawi yawo ndi malo, koma munthawi yotsiriza, iwo onse akuomba kupyolera mwa wanthenga wa mpingo wa m'bado wa chisanu ndi chiwiri **kachiwiri.** Izo zinatsiriza "chinsinsi" cha Chivumbulutso, 10:7. Taonani, kutinso pa vesi 11 la chaputala ichi…,Yohane, amene ndi woimirira Mkwatibwi ndi utumiki [iye anaimirira ziwiri] akuuzidwa kuti anenerenso pa maso pa anthu onse, mafuko, zilankhulo, ndi mafumu. Izi zikuonetsera kuti ntchito ya munthawi yotsiriza ya utumiki uwu, mabingu atalankhula mau awo potsiriza zisindikizo, ndi umboni padziko lonse.

Mu 1963, pamene Mulungu analankhula ndi M'bale William Branham pazokhudza zisindikizo zisanu ndi ziwiri. Iye anauzidwa mu masomphenya kuti apite ku madzulo [iye amakhala ku Indiana] kukakumana ndi angelo asanu ndi awiri amene adali ndi zisindikizo. Iye anachita ichi. Kotero iye atabwerera ku Indiana kukalalikira zisindikizo zisanu ndi ziwiri, aliyense wa angelo asanu ndi awiri amaulura chisindikizo kwa iye. Mngelo wauzimu wachisanu ndi chiwiri amene anali ndi chisindikizo chachisanu ndi chiwiri amatanthauza zochuluka kwa m'bale Branham, kusiyana ndi ena mwa angelo aja. Pamene angelo anabwera **wachisanu ndi chiwiri anaulukira molunjika kwa m'bale Branham, amene anali wanthenga wa m'bado wachisanu ndi chiwiri.** Izi zinakwaniritsa gawo lapadera la utumiki wa m'bale Branham, chifukwa nthawi iyi isanafike Mulungu anali atamuuza iye kuti padzakhala magawo atatu, kapena zikoka, kuutumiki uwu. Pofuna kusiyanitsa pakati pa zikoka, Mulungu anamuonetsa iye masomphenya a kagulu ka mbalame zazing'ono, zimene zinaimirira chikoka choyamba. Ku chikoka chawiri iye anaonetseredwa gulu lokulirapo la mbalame ngati nkhunda. Pamene Mulungu anamuonetsera chimene chimaimirira chikoka chachitatu, iye adaona angelo asanu ndi awiri awa ku bukhu la Chivumbulutso, iwo adalankhula mau awo kupyolera mwa mneneri, ndiye kutsiriza zisindikizo zisanu ndi ziwiri **zonse.**

Pansi pa chikoka choyamba m'bale Branham amatha kutenga anthu pa dzanja ndikuwafotokozera chimene chinali vuto lawo, ndipo ambiri anachiritsidwa, pamene amapemphera nao. Pansi pa chikoka chachiwiri iye amatha kudziwa malingaliro awo ndi kuwauza anthu vuto lawo, kapena chimene amafuna, posawatenga iwo padzanja. Izi zinakweza mochuluka chikhulupiriro chawo ndipo ambiri anapulumutsidwa ku chimene chimavuta. Pansi pa chikoka chachitatu m'bale Branham amatha kulankhula mau, ndipo chilichonse chimene amadzozedwa kulankhula chimachitika. Uwu ndi utumiki umene angelo asanu ndi awiri amaimirira. Izi ndi zofunika kwambiri mu chaputala ichi, chifukwa angelo asanu ndi awiri **omwewo** amene anabwera kwa m'bale Branham ndi angelo omwewo asanu ndi awiri amene akuonetseredwa mu chaputala ichi. Pansi pa chili chonse cha zikoka izi mau a Mulungu amalalikidwa, zimangobwera mochuluka ndi chikoka chili chonse.

CHIFUKWA CHIMENE INE NDIKUBWERETSERA UTUMIKI WA M'BALE BRANHAM NDI CHOTI UTUMIKI WA CHIKOKA CHACHITATU UWU UMENE UNAONETSEREDWA MU CHAPUTALA CHAKHUMI CHA CHIVUMBULUTSO, VESI 8-11.., KUNGOTI PANO NDI UTUMIKI USANU WA AEFESO 4:11-16, UMENE UKUTENGA UTUMIKI UWU.

Pa mfundo iyi, ife tikuyenera kuona mfundo yoti m'bale Branham anali ndi mzimu wa Eliya pa iye ndipo kuti utumiki wake sunali wa mtundu wa Aefeso 4:11. **Mu dongosolo la utumiki usanu mneneri wa ku Chipangano Chatsopano ali wachiwiri kwa mtumwi.** Kotero, pofuna kumupatsa m'bale Branham malo ake m'malemba, ife tikuyenera kumuona iye ngati Eliya amene walankhulidwa ku Malaki 4:5-6 [kukwaniritsa Gawo B; Yohane m'batizi kukwaniritsa Gawo A.]. Kumeneko ndi kubwezeretsa mpingo ku kachitidwe ka mpingo wa pachiyambi. Iye

sanatumizidwe kuti afikitse oyeramtima ku umgwiro; izi ndi za utumiki usanu wa pa Aefeso 4:11. Izi sizikanagwira ntchito kufikira mneneri atafa, m'bale William Branham. Ngati utumiki wa Chipangano Chatsopano ukanati ukhale mudongosolo m'bale Branham alipo, iye akanakhala wachiwiri mu utumiki ndipo pokhala wachiwiri, iye sakanakhala wanthenga ku m'bado. Koma pamene tiona kuti anali mneneri mu dongosolo la Chipangano Chorale; kotero ife tikhoza kumuika iye mu malemba molondora. Tsopano ife tikhoza kumvetsa chimene Mulungu anachita potitumizira ife Eliya mneneri, pano mu nthawi yotsiriza.

DONGOSOLO LA CHIPANGANO CHATSOPANO la utumiki ndi choyamba atumwi, kachiwiri aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi, ndipo ili ndi dongosolo la uzimu la utumiki wa Chipangano Chatsopano.

Ku Chipangano Chakale, Mulungu anachita mochuluka mu gawo logwiritsa ntchito munthu mmodzi pa nthawi kubweretsa Mau ake kwa anthu. Izi zikutero pa chifukwa chakuti, [ngakhale kuti utumikiwa ku Chipangano Chatsopano ndi utumiki usanu ndipo osati utumiki wa munthu m'modzi monga ku Chipangano Chakale], m'bale Branham anati nthawi zambiri kuti Mau amabwera kwa mneneri yekha, ndi kuti Mulungu amagwiritsa ntchito munthu m'modzi pa nthawi imodzi. Mopanda kumvetsa kwenikweni zimenezi zikanatha kukhala zotsutsana kwa thunthu ndi malemba. Koma pomvetsa bwino malemba, komanso pokhala ndi kumvetsa kuti kagawo ka utumiki wa Chipangano Chakale unaonekera mwa m'bale Branham, izi zimatipanga ife kudziwa kuti ananena zimenezo chifukwa iye anali ndi mzimu wa Eliya, mzimu wa mneneri wa ku Chipangano Chakale, pa iye. Kotero, pokhala mzimu wa Eliya unali pa iye, kulankhula kumeneko, kumene kukanatha kukhala kotsutsana ndi malemba, makamaka kwa iye amene ali mu utumiki usanu kuti anene. Koma tsopano amakuza malemba pamene akulankhulidwa ndikugwiritsidwa ntchito, m'bale Branham amene utumiki wake unali wa Chipangano Chakale.

Izi zikutibweretsa ife mu nthawi ku malo, kumene Mulungu wayamba kuika utumiki wa ku Chipangano Chatsopano monga mpingo oyamba unaliri. Mulungu anamulora m'bale Branham kuona mokwanira za zimene zidzachitike pamene zisindikizo zimauluridwa, kutipanga kuti tidziwe kuti Khristu adzakhala padziko kugwira ntchito ndi Mkwatibwi wake wokhala ndi mamembala ambiri. Izi ndi kumufikitsa Iye ku ungwiro kukonzekera Mkwatulo.

Taonaninso pamene mabingu adalankhula mu tsiku la Yohane, iye adamvetsa bwinobwino zimene zinalankhulidwa ndipo amafuna kuti alembe zimene zinalankhulidwa, koma anauzidwa kuti asalembe. M'malo mwake, iye amayenera kusindikiza ndi zisindikizo zisanu ndi ziwiri, koma tsopano tithokoze Mulungu, kuti zisindikizo zachotsedwa ndipo bukhu latsegulidwa pano mu nthawi yotsiriza koma kwa mkwatibwi wa Khristu yekha.

Ine ndikufuna ndipitirize ndi chaputala ichi pogawa magawo anai. Vesi 1-4 ndi gawo loyamba, ndipo ndi kubwera kwa Khristu mu maonekedwe amngelo, komanso kuonetsa mabingu kulankhula mau awo. Vesi 5 ndi 6 ndi gawo lachiwiri, ndipo likuchita ndi kulengeza kuti *"sipadzakhalanso nthawi"* kwa mabungwe azipembedzo. Vesi 7 ndi gawo lachitatu, ndipo likukhudzana ndi wanthenga wa m'bado wa mpingo wa chisanu ndi chiwiri ndi chimene uthenga wake wakwaniritsa. Vesi 8-11 ndi gawo lachinai, ndipo likuchita ndi uthenga umene ukulalikidwa kwa mkwatibwi amene watulutsidwa kuzipembedzo ndi wanthenga wa m'bado wachisanu ndi chiwiri. Tsopano Mulungu atithandize pamene tikuwerenga malemba.

Gawo Loyamba

Vesi 1*: "Ndipo ndinaona mngelo wina wolimba alikutsika kuchokera kumwamba, wovala mtambo; ndi utawaleza pa mutu pache, ndipo nkhope yake ngati dzuwa ndi mapazi ache ngati mizati yamoto."*

Vesi 2: *"Ndipo anali nako m'dzanja lake kabukhu kofunyulula; ndipo anaponda nalo phazi lake lamanja pa nyanja."*

Vesi 3: *"Ndi lamanzerero pa mtunda, napfuula ndi mau akulu, monga ngati mkango ubangula; ndipo pamene anapfuula mabingu asanu ndi awiri analankhula mau awo."*

Vesi 4: *"Ndipo pamene adalankhula mabingu asanu ndi awiriwo ndinati ndilembe; ndipo ndinamva mau ochokera kumwamba nanena, sindikiza nacho chizindikiro zimene adalankhula mabingu asanu ndi limodzi, ndipo usazilembe."*

Awa ndi masomphenya. Yohane adaona mngelo wankulu akutsika kuchokera kumwamba. Kwenikweni, mngelo anali wankulu mumaonekedwe a m'masomphenya moti dziko lapansi limaoneka lochepa, koma iye anaika phazi limodzi pa nyanja ndi phazi limodzi pa dziko; komanso taonani, bukhu lopfunyulura lotseguka mu dzanja Lake lamanja.

Makamaka, palibe bukhu logwirika. Yohane sakanatha kuona zimene zinali mu malingaliro a Mulungu, kotero Mulungu adamulora iye kuona bukhu kuti akathe kupereka malingaliro ake kwa ife. Ndi kumvetsa pa zimene mtumwi Paulo amatanthauza poika zimene amatanthauza poika zimene amalankhula. **"Tanthauzolo" ndi limene linasindikizidwa, chifukwa tinali kale ndi chimene adanena** {mau olembedwa] **zisindikizo ndi bukhu zisanatsegulidwe. Tsopano tili nako kumvetsa. Mngelo Wankulu** [amene ndi Mzimu] **akhoza kungobweretsa bukhu la uzimu, kotero ndi "kumvetsa" kumene tikukuona mu dzanja lamanja la mngelo. Yohane amayenera kuona ilo ngati bukhu lenileni, poti kunali kosatheka kuona "kumvetsa."**

Pachiyambi cha mpingo, Paulo amatha kutchula iwo amene maina awo anali mu bukhu la moyo pa chimene anakhulupirira. Izi zalembedwa ku Afillipi 4:3. Paulo anati, *"Antchito amzanga, amene maina awo ali mu bukhu la moyo."* Izi zikuonetsera kuti zimene mumakhulupirira zimaonetsera ngati muli mu malingaliro a Mulungu kapena ayi. Mu 1 Akorinto 1:10, Paulo akuuza Mpingo kuti *"mumangike mu mtima womwewo ndi mchiweruzo chomwecho."* Mwa kulankhula kwina, aliyense adzakhulupirira uthenga womwewu ndi kutsatira vumbulutso lomweli mu nthawi yotsiriza, ngati maina awo ali mu bukhu la moyo, monga m'mene anatsatira zimene mtumwi Paulo anaphunzitsira. Zikuyenera kukhala zimodzi tsopano.

Mtambo, utawaleza, nkhope ngati dzuwa, ndi mapazi ngati mizati ya moto, zikutiuza chimene iye ali. Iye ndi Yesu Khristu mu vumbulutso, mu maonekedwe auzimu kubwera ku dziko Mkwatulo usanachitike. **Iye wavala mtambo kudziphimba kwa iwo amene sanadzozedwe kuti asamuone Iye.** Izi ndi zoona mwapadera mu tsiku lotsiriza ili, pamene Mkwatibwi yekhayo woona adzadziwa chimene chikuchitika. *"Nkhope yake inawala ngati dzuwa,"* tiyeni tione kuti ngakhale Iye waphimbika ndi mtambo, iwo amene ali ndi vumbulutso akhoza kumuona bwinobwino. Zili ngati m'mene zinaliri mu masiku amene Yesu anayenda pano mu thupi la munthu. **Iye amalankhula mu mafanizo kupanga mtambo wauzimu kuzibisa yekha kwa onse kupatula osankhidwa;** koma kwa Petro nkhope yake imaoneka ngati dzuwa pamene iye anati, *"Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wa moyo."* Yesu anadziwa kuti njira yokhayo Petro akanatha kudziwa izi anali Mulungu kumuonetsera iye. Yesu anali atavala mtambo wauzimu ndipo okhawo amene anali ndi vumbulutso loperekedwa ndi Mulungu akanatha kudziwa kuti Iye anali yani ndi kuona "Nkhope Yake inali ngati dzuwa." Ndi chinthu

chomwecho lero! Yesu anati ku Mateyu 16:17-18 [mongotchula] kuti thupi ndi mwazi sizinaulure "Nkhope ngati dzuwa," koma Atate wanga amene ali kumwamba waulura icho kwa iwe. Yesu anati "pa vumbulutso ili" Ine ndidzamanga mpingo wanga ndipo zipata za Gehena [mipingo yopanda vumbulutso ya zipembedzo] suzaulaka. Chifukwa chiyani? Ndi chifukwa chakuti Mkwatibwi ali ndi vumbulutso kuchokera kwa Mulungu ndipo palibe chimene chingamulepheretse kuchita chifuniro cha Mulungu.

Chinthu chinanso pa *"kuvala mtambo"* ndi *"ndipo nkhope yake ngati dzuwa."* Nkhope yake inawala ngati dzuwa kwambiri mu bukhu la Machitidwe kusiyana ndi m'mene inachitira nthawi iliyonse mbuyomu, chifukwa odwala ambiri anachiritsidwa pamene nthunzi wa Petro umadutsa pa iwo. [Machitidwe 5:15] komanso Machidwe 5:16 akuti, *"ndipo anachiritsidwa yense wa iwo."* Koma mu tsiku lotsiriza ili Khristu wabwera wophimbika mu mtambo, ndipo Iye wabisika kwa opanda vumbulutso…, koma kwa Mkwatibwi, nkhope yake *"ikuwala ngati dzuwa."* Nkhope yake kwenikweni "inawala ngati dzuwa, mu utumiki wa m'bale Branham.

Mngelo Wankulu uyu ali ndi utawereza pa mutu wake, kusonyeza kuti Iye akubwera ku dziko ndi Pangano Latsopano la Mulungu, yotumikiridwa ndi utumiki usanu. Ichi ndi chifukwa chake utawaleza uli pa mutu pake.

Tsopano, mapazi ngati mizati yamoto: Mizati yamoto ikuonetsera kukhalapo kwa Khristu pa dziko.

Taonani, vesi 1-4 ikuonetsera Khristu akubweranso ku dziko mu maonekedwe a mngelo. Iye atangofika akupfuula ndi mau akulu ngati Mkango wobangula. Izi zikutidziwitsa kuti chiombolo chatha mu "chikhalidwe cha m'bado wa mpingo," ndipo Iye wabwera kwa Mkwatibwi wake.

Tsopano, ife timafika pamalo pamene vumbulutso la mabingu asanu ndi awiri ikuonetseredwa kukhala vumbulutso la zisindikizo zisanu ndi ziwiri. **MABINGU NDI ANGELO ASANU NDI AWIRI AUZIMU AMENE ANAGWIRA NTCHITO NDI KHRISTU KUDUTSA MU MIBADO ISANU NDI IWIRI YA MPINGO.** Kotero chinsinsi cha mabingu si chimene iwo ali, izo ndi zomveka. Chinsinsi ndi *zimene analankhula* mau awo auzimu kupyolera mwa liu la padziko la wanthenga wa m'bado wa mpingo wa chisanu ndi chiwiri; ndipo tsopano tikudziwa kuti zikugwirizana ndi mibado isanu ndi iwiri ya mpingo imene tadutsamo, ndipo yatsirizidwa ndi mabingu asanu ndi awiri.

MAU A MPHAMVU A KHRISTU NDI MAU A ANGELO ASANU NDI AWIRI OTHANDIZIRA AKUPANGA KUONEKA BUKHU LA CHIVUMBULUTSO POULURA ZISINDIKIZO ZISANU NDI ZIWIRI. Ichi ndicho chifukwa utumiki wa Aefeso 4:11 ukubweretsedwa mu dongosolo la uzimu, pamene Khristu ali pano kudzavomereza mau amene akulankhulidwa ndi utumiki wamoyo. Izi zidzabweretsanso kukwaniritsidwa kwa 1 Akorinto 1:10, onse akulankhula chinthu chimodzi, koma Yohane anauzidwa kuti asalembe zimene zinalankhulidwa, koma tithokoze Mulungu kuti zaululidwa mwa kutsegulidwa kwa **zisindikizo zisanu ndi ziwiri.**

Gawo Lachiwiri

Gawo lachiwiri la chaputala ichi ndi Mngelo Wankulu akutiuza ife kuti nthawi yatha ya kachitidwe aka ka zipembedzo.

Vesi 5: *"Ndipo mngelo amene ndinamuona ali kuimirira pa nyanja ndi pamtunda, anakweza dzanja lake lamanja kuloza kumwamba."*

Vesi 6: *"Nalumbira kutchula Iye amene ali ndi moyo ku nthawi za nthawi, amene adalenga m'mwamba ndi zinthu ziri momwemo, ndi dziko lapansi ndi zinthu zili momwemo, ndi nyanja ndi zinthu zili momwemo kuti sipadzakhalanso nthawi."*

Chivumbulutso 2:18-23 chikuchita ndi Yezebeli amene ndi mpingo wa Katolika, mai wa mahule. Baibulo likuti iye anapatsidwa nthawi kuti alape, koma sanalape. Iye anachita chigololo ndipo ana anabadwa a iye. Mulungu anati iye adzapha ana ake [mipingo ya chiprotestant] ndi imfa. Ndi chimene vesi 5 ndi 6 ikutanthauza.

Werengani mwa pemphero tsopano, *"sipadzakhalanso nthawi"* akuti palibenso chifundo ku kachitidwe ka zipembedzo monga zinaliri mu nthawi ya m'bado wotsiriza uwu. **Palibenso kachitidwe ka chipembedzo padziko kamene kali ndi madalitso a Mulungu pa iwo mu nthawi ino.** Moyo wa Mulungu unali mu kachitidwe ka zipembedzo mu mibado ya mpingo, ndipo Mulungu analora tirigu ndi nansongole kukula palimodzi monga Mateyu 13 akutiuza, koma tsiku limenelo latha ndithu pamene chaputala ichi chikukwaniritsidwa. Khristu akulumbira kuti "palibenso nthawi" kapena kuti nansongole ndi tirigu sangakulirenso palimodzi. Kumasulira kwina kukuti "nthawi siyidzachedwetsedwanso." Mwa kulankhula kwina Iye sakuchitanso mu gawo la chikhristu. Iye tsopano akufikitsa Mkwatibwi wake ku ungwiro, monga onse a iwo [Mkwatibwi] adzatulutsidwa mu mabungwe a zipembedzo pamene nthawi iyi ikutha.

Atatha Khristu, amene ndi Mau odzozedwa, kuchoka mu kachitidwe ka zipembedzo, iwo anasandulika mokhalamo ziwanda. Pofika pakati pa sabata la 70 la Danieli, adierekezi adzakhala atatenga kwathunthu kachitidwe konse ka mpingo, monga Chivumbulutso chaputala 18 chikuonetsera.

Mulungu anatumiza wanthenga wa m'bado wa mpingo wachisanu ndi chiwiri ndipo iye analalikira Mau a Mulungu, mipingo ya chipembedzo inakana ndikuzikankhira uko. Kenako Mngelo Wankulu anabwera pomwepo ndi wanthenga wa m'bado wa mpingo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri, ndikukweza dzanja lake kumwamba ndi kunena, "sikudzakhalanso nthawi" kwa Chikatolika komanso Chiprotestant. Kotero, ndi zabwino kulalikira "Tulukani m'menemo anthu anga." Iye sali bwino. Iye ndi wonyansa. Iye ndi wakugwa, izi zikutanthauza kachitidwe konse ka mpingo. Uku ndikutanthauza kwa vesi 5 ndi vesi 6, ndi gawo lachiwiri la chaputala ichi.

Gawo Lachitatu

Vesi 7: *"Komatu m'masiku a Mau a mngelo wachisanu ndi chiwiri m'mene iye adzayamba kuomba, pamenepo padzatsirizika chinsinsi cha Mulungu, monga analalikira* [kapena ndi] *kwa akapolo ache aneneri."*

Ili ndi gawo lachitatu la chaputala cha khumi. *"Komatu m'masiku a mau,"* kodi zimenezo zikutiuza ife chiyani? Mu zochitika zikuti, "Pamene mau a mngelo wachisanu ndi chiwiri anali pano." Ife tikanati, "Mu masiku amene mngelo wachisanu ndi chiwiri anaomba mau ake kuchokera ku Jeffersonville, Indiana, U.S.A," iye anatenga Baibulo ndipo mwakuthandizidwa ndi Mzimu Woyera ndi angelo auzimu asanu ndi awiri, anaulura chinsinsi cha zisindikizo zimenezo. Iye anatenga Baibulo ndikutionetsera ife chimene mibado isanu ndi iwiri ya mpingo inali.

Kodi chinsinsi cha Mulungu ndi chiyani? Mngelo wachisanu ndi chiwiri anatsiriza chinsinsi chimene chinalankhulidwa ndi akapolo, aneneri, chimene chimakhudza zinsinsi zimene zinali mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Mau a mngelo wachisanu ndi chiwiri wauzimu anaomba kupyolera mwa m'bale Branham, [nyenyezi] ya pansipano yachisanu ndi chiwiri, ndi

kumuonetsera iye chimene zisindikizo zinali. Izo zinauluridwa, ndipo zinafanizidwa ndi mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Paulo analinso ndi "chinsinsi" kuulura mu tsiku lake. "Chinsinsi" chimenecho chimayenera kuchita ndi Amitundu kuvomerezedwa mu mpingo wa chiyuda [Aefeso 3:1-9], ndipo ndi "chinsinsi" chosiyana ndi cha pa Chivumbulutso, chaputala 10:7. Amitundu kuikidwa mu banja la Mulungu pamodzi ndi Ayuda chinali **"Chinsinsi Chao,"** chimene Paulo anaulura. Koma chinsinsi ku Chivumbulutso chaputala 10:7 chinali njira imene mpingo unadutsamo kwa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo ndipo chimenecho ndi **"Chinsinsi Chathu."**

Aneneri a ku Chipangano Chakale amene adalankhula mu nthawi yakale yaku Chipangano Chakale anaonetsera mu malo osiyanasiyana mu Chipangano Chakale, kuti Mulungu adzaonetsera chifundo kwa Amitundu. Mulungu amadziwa kuti Ayuda adzamukana, ndipo nthambi yachilengedwe idzadulidwa, ndipo Amitundu adzalumikizidwa ndi kukhala otenga gawo a uthenga. Iwo analankhula mwa chinsinsi koma Paulo anatsiriza chinsinsi chimenechi, monga m'mene mngelo wachisanu ndi chiwiri anatsiriza chinsinsi cha m'bado wa mpingo. **Kuomba kwa m'bale William Branham kwapangitsa zinsinsi za mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo kudziwika, pamene zisindikizo zimauluridwa.** Mau a mneneri aonetsera njira imene mpingo watenga kuchokera pa pentekosite mpakana pano. Chinsinsi ichi cholankhulidwa pa vesi 7 chadziwika kale kwa Mkwatibwi wa Khristu, ndipo ndi chinsinsi chomwecho chimene Yohane analemba mu chaputala choyamba cha Chivumbulutso, vesi 20. Apa Yohane akuuzidwa za chinsinsi, "chinsinsi chimodzi," chimene chimachita ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri za golide ndi mipingo isanu ndi iwiri imene anaiona. Ichi ndi chinsinsi chimene chinaululidwa ndi wanthenga wachisanu ndi chiwiri. Ngakhale Mulungu anagwiritsa ntchito iye kuulura zinsinsi zina…, mosakaika, chinsinsi chimodzi chimene chikulankhulidwa pa vesi 7 la chaputala ichi, ndi chimene Yohane anaona ngati chinsinsi chimodzi, ndipo chadziwika kwa ife ndi mneneri wa Mulungu wanthenga wa m'bado wa Laodikaya. Tsopano, izi ndi zomveka kwa ife.

Gawo Lachinai

Tsopano tikupita ku gawo lachinai la chaputala ichi. Mwachidule ndi uthenga umene unalalikidwa ndi mtumwi Paulo kubwezeretsedwanso, ndi kumvetsa kumene kunataika mu mpingo woyamba. Khristu kubweretsanso chimene chinalankhulidwa, kwa Mkwatibwi wake kupyolera mu utumiki usanu, monga Khristu tsopano wamupatsa iye utsogoleri wa utumwi.

Vesi 8: *"Ndipo mau ndinawamva ochokera kumwamba, anankhulanso nane, nanena, muka tenga bukhu lofunyuluralo m'dzanja la mngelo wakuimirira panyanja ndi padziko."*

Vesi 9: *"Ndipo ndinamva kwa mngelo, ndi kunena naye, ndipatse kabukhuko. Ndipo ananena ndi ine, Dzatenge, nudye; ndipo kadzawawitsa m'mimba mwako, komatu mkamwa mwako kadzazuna ngati uchi."*

Vesi 10: *"Ndipo ndinatenga kabukhu mu dzanja la mngelo, ndipo ndinakadya; ndipo kanali mkamwa mwanga kozuna ngati uchi, ndipo pamene ndinakadya m'mimba mwamba mudawawa."*

Vesi 11: *"Ndipo adanena nane, uyenera iwe kunenera iwe kuneneranso pa anthu ndi mitundu, ndi manenedwe, ndi mafumu ambiri."*

Taonani kuti mau a vumbulutso anayamba kulankhula ndi Yohane. **Awa ndi mau a mzimu wamuyaya pamene Iye akulankhula kupyolera mwa munthu Khristu Yesu amene akukhalabe pa mpando wa chifumu kumwamba, pamene utumiki uwu ukukwaniritsidwa**

mpakana nthawi ya Mkwatulo. Yohane ndi woimirira wa utumiki woona, ndipo utumiki woona ndi gawo la Mkwatibwi. Mau a Mulungu akulankhulabe wanthenga wa m'bado wa mpingo wa chisanu ndi chiwiri, atapita kuitanidwa kumudzi, kuonetsera kuti Mulungu akulankhulabe kwa Mkwatibwi wa Khristu kupyolera mu utumiki usanu.

Taonani m'mene Mzimu wa Mulungu umalankhulira ku mpingo. Ngati inu muli Mkwatibwi wa Khristu mu nthawi ino…, kotero Mzimu wa Mulungu akulankhula ndi inu, ndikuti, "Pitani tengani chakudya icho mudzanja la mtumiki, monga m'mene mpingo wakerle unachitira. Pitani mutenge kabukhu kakang'ono ndipo mukhale ngati mpingo woyamba, umene unali pansi pa utsogoleri wa mtumwi Paulo."

Ndilozuna mkamwa mwako, koma pamene lilowa m'mimba mwako limawawa. Limangofuna iwe kuti uchoke pakati pa dziko lapansi ndi pakati pa zipembedzo.

Tsopano, kodi mukuona chimene mngelo ali amene wabweranso ku Chivumbulutso, chaputala 10? Ndi Khristu mu maonekedwe a mngelo kubwera mu chidzalo chake kwa Mkwatibwi wa Khristu, kumukonzekeretsa Mkwatulo.

Mabingu asanu ndi iwiri NDI angelo asanu ndi awiri auzimu amene amathandiza Khristu, pamene Iye akubweranso ku dziko mu maonekedwe a mngelo. Bukhu laling'ono [lopfunyulura] ndilowawa m'mimba. Mu m'bado wa Laodikaya, *"ufulu wa anthu,"* ambiri akufuna njira zao, koma Mkwatibwi adzatsatira utsogoleri wa Mulungu ngakhale zitanthauze kumeza zapamtima zao.

Kotero Mkwatibwi adzapitirira kuwerenga Baibulo lake ndi kumanga maziko amenewo. Tengani zimene Paulo adanena ndi kupanga Khristu mwa inu. Petro amadutsa m'menemo pamene iye anati kutenga chilengedwe chauzimu kupangidwa mwa inu. [2Petro 1:1-8] **Komanso, 2 Petro 1:19 akutiuza za nyenyezi ya tsiku latsopano.**

Komanso, kuikidwa kwa **ponseponse kwa utumiki usanu ndi kwa anthu ambiri, mafuko, manenedwe ndi mafumu** [kapena maufumu]. Utumiki uwu [wa vesi 8-11 wa chaputala ichi] ndi kunenera, chimene chikutanthawuza kuti kulalikira kwao ndi **"kulalikira kwa vumbulutso lakuya"** zimenezo ndi kwa Mkwatibwi ku mafuko onse, ndipo iye adzamvetsa mwangwiro. Zimenezo tsopano zikuchitika kupyolera mu utsogoleri wa utumwi! Ndipo potsiriza pa utumiki uwu, Mkwatulo ukuchitika pamene aneneri awiri apita ku Israeli. Chaputala cha khumi ichi tsopano chasandulika "chowala ngati khrustalo." Amen

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHIMODZI

Vesi 1: *"Ndipo anandipatsa ine bango ngati ndodo, ndi kuti, Tanyamuka, nuyese Kachisi wa Mulungu, ndi guwa la msembe, ndi iwo akulambiramo."*

Vesi 2: *"Ndipo bwalo la kunja kwa Kachisi uliyese padera, osaliyesa, pakuti adapatsa ilo kwa amitundu; ndipo mzinda wopatulika adzaupondereza miyezi makumi anai mphambu awiri."*

Mngelo anati *"yesa kachisi wa Mulungu, ndi guwa la msembe, ndi iwo akulambiramo*." Pakali pano kachisi wa Chisilamu wamangidwa pa guwa penipeni pamene padzakhale pakumangidwanso kwa kachisi wachiyuda. Ndi njira ya Mulungu yowalepheretsa Ayuda kumanga kachisi kufikira nthawi yake yeniyeni, cha kumayambiriro kwa sabata la 70 la Danieli.

Mngelo uyu akuuza Yohane kuti adzuke ndi kuyeza, ngakhale kuti kachisi anali kale ataonongedwa. Masomphenya awa ndi mu 96A.D, ndipo kachisi anagwetsedwa ndi Tito mu 70 A.D. Yohane ali mu masomphenya kuona kachisi akumangidwanso. Masomphenya awa akutiuza kuti padzakhala kachisi wina kumangidwanso mu tsiku lotsiriza mu Yerusalemu

pamalo pomwepo pamene wakale anali zisanachitike mu 70A.D. Yohane anaziona izi mumasomphenya, zimakwanira. Kachisi adzamangidwanso cha kumayambiriro a sabata la 70 la Danieli. Ndionjezerepo apa kuti kachisi sadzatsirizidwa nthawi iyi kuti agwiritsidwe ntchito.

Tayang'anani kuti kachisi anamangidwa, guwa linamangidwa ndipo Yohane anauzidwa kuti ayeze iwo, koma anauzidwa kuti asayeze bwalo limene linali kunja kwa kachisi, chifukwa linapatsidwa kwa Amitundu. Izi zikutionetsa kuti amitundu adzaponda pa mzinda woyera kwa miyezi makumi anai ndi iwiri. Zimenezo ndi zaka zitatu ndi theka za sabata la 70 la Danieli, kapena nyengo ya chisautso chachikulu chimene chikubwera padziko lapansi.

Pamene tikupitirira mu chaputala ichi, kumbukirani kuti chinthu choyamba chimene Yohane anachiona chinali kachisi amene anamangidwa. Chinthu chachiwiri chimene anachiona, chimene chinamuzindikiritsa kuti uyu ndi kachisi kumangidwanso chinali guwa. Zimamveka ngati guwa limeneli ndi nthanthwe limene Abrahamu anatsala pang'ono kuperekerapo msembe mwana wake. Kotero kachisi ameneyo adzamangidwanso mu tsiku lotsiriza ili.

Chinachake chichitika ku Israeli ndipo Israeli adzatenganso malo omwewo. Iwo adzamanga kachisi ndi kuperekanso msembe mu gawo loyamba la sabata la 70 la Danieli monga m'mene anachitira ku Chipangano Chakale, koma padzakhala gulu limene lidzazindikira msembe yeniyeni, Yesu Khristu, ndi kusindikizidwa ndi chisindikizo cha Mulungu mu tsiku ili lotsiriza. [Chivumbulutso 7]

Chinthu china chimene ndikufuna kuti inu muone ndi chakuti pamene kachisi akumangidwa pali aneneri awiri poyera. Aneneri awiri amenewo adzakhala ndi mzimu wa Mose ndi Eliya pa iwo. Mzimu wa Mose ndi Eliya ukubweranso mu tsiku lotsiriza pa Ayuda awiri.

Vesi 3: *"Ndipo ndidzalamulira mboni zanga ziwiri, ndipo zidzanenera masiku chikwi chimodzi ndi mazana awiri mphambu makumi asanu ndi limodzi, zovala chiguduli."*

Vesi 4: *"Izo ndizo mitengo iwiri ya Azitona ndi zoikapo nyali ziwiri zakuima pamaso pa Ambuye wa dziko lapansi."*

Vesi 5: *"Ndipo wina akafuna kuipsa izo, moto utuluka mkamwa mwao, nuononga adani awo; ndipo wina akafuana kuipsa izo, maphedwe ache ayenera kutero."*

Vesi 6: *"Izo zili nao ulamuliro wakutseka m'mwamba, isagwe mvula masiku a chinenero chao, ndipo ulamuliro ziri nao pamadzi kuwasandutsa mwazi, ndi kupanda dziko ndi mliri uli wonse zikafuna."*

Kumbukirani m'mene tinaphunzirira malipenga mu chaputala cha chisanu ndi chitatu. Lipenga loyamba linaomba, panalibe mvula, ndipo panalibe chilala, ndi zina zotero. Uwu ndi uthenga wa aneneri awiri. Pansi pa lipenga lachiwiri madzi anasandulika magazi. Iwo sanatseka kumwamba kokha kuti mvula isagwe, iwo sanangosandutsa madzi magazi, koma nakantha dziko ndi miliri pafupipafupi monga anafunira, monga anafunira, monga Mose anachitira ku Aigupto. Mulungu anaikiza mwa aneneri awiri amenewa mphamvu zazikulu, chifukwa ali ndi ntchito yoti agwire. Iwo akuyenera kuitana Ayuda 144,000 ndi kuwasindikiza mu gawo loyamba la sabata la 70 la Danieli.

Tiyeni tione mbuyo mu nthawi ya Haggai ndi Zakaria pamene kachisi wachiwiri amamangidwa, chifukwa chinthu chomwecho chinachitika mu tsiku limenelo monga zidzachitikire m'tsogolomu. Ine ndikufuna inu kuti muone kugwedeza kumene kunachitika ndi aneneri awiri poyera pamene kachisi amamangidwa.

Tiyeni tione mbuyo ku Haggai ndi Zakaria ndipo kenako tibweranso ku chaputala cha khumi ndi chimodzi cha Chivumbulutso ndi kuona ngati zikumveka kwa inu. Pali ma chaputala awiri okha mu bukhu la Haggai ndipo akufotokoza za kumanganso kwa kachisi. Yerusalemu anapita ku ukapolo. Ayuda anatengedwa kupita Babulo ndipo Mulungu adawalora kubwereranso ndi

kumanganso kachisi. Ine ndikufuna kuti inu mudziwe kuti panali aneneri a Chiyuda awiri poyera pamene kachisi amamangidwa. **Mulungu nthawi zonse amatumiza aneneri achiyuda pamene Iye akufuna kuti anenere kwa Ayuda.** Ilo ndi dongosolo la Mulungu, ndipo apa Iye ali ndi aneneri awiri poyera kunenera pamene kachisi akumangidwanso. Chinthu chofanana chidzachitika mu tsiku lotsiriza. Aneneri awiri amenewo anali Haggai ndi Zakaria.

Tiyeni tibwerere ku nthawi ya Haggai ndi Zakaria pamene kachisi amamangidwa, chifukwa chinthu chofanana chinachitika mu tsiku limenelo monga zidzachitikire mtsogolo. Ine ndikufuna kuti muone kugwedeza kumene kunachitika ndi aneneri awiri poyera pamene kachisi wachiwiri amamangidwa.

Tiyeni tiwerenge ku chaputala choyamba cha Haggai, vesi 2 ndi 8. Iwo abwerera ku dziko atakhala ku Babulo ku ukapolo kwa zaka makumi asanu ndi awiri, ndipo Mulungu akuti amange kachisi. Haggai 1:2- *"Atero Yehova wa makamu, akuti, Anthu awa anena, Nthawi siinafike, Nthawi yakumanga nyumba ya Yehova."*

Anthu lero sangathe kulingalira kuti nthawi ya Mulungu ndi iyi ndi kuti nthawi ya Mulungu siiyi. Apa, anthu amanena kuti iyi sinthawi yomanga nyumba ya Ambuye. Mulungu anatumiza aneneri awiri kuwagwedeza anthu. Haggai 1:8- *"Kwerani ku dziko la mapiri, ndi kukwera nayo mitengo, mumange nyumbayi, ndipo kudzandikomera, ndipo ndidzalemekezedwa ati Yehova."*

Anthu anamanga nyumba zawo, koma sanamanga nyumba ya Mulungu. Mulungu anayamba kuwauza iwo kuti inali nthawi yomanga nyumba ya Ambuye. Nthawi zonse zimatengera mneneri kudzutsa Israeli.

Tiyeni tipite ku chaputala 2. Haggai 2:3- *"Adatsala ndani mwa inu amene anaona nyumba iyi mu ulemerero wache woyamba? Ndipo muyiona yotani tsopano? Kodi siikhala m'maso mwanu ngati chabe?"*

Nyumba yoyamba imene Solomo adamanga inali chinthu chapamwamba, koma kachisi uyu sanali wankulu kapena wapamwamba ngati amene Solomoni adamanga, koma Mulungu amafuna kuti amangidwe kukwaniritsa Mau ake. Ambiri a anthu akale amene amabwerera ku dziko la kwawo amatha kukumbukira kachisi woyamba. Iwo anati kuti kachisi sanali kanthu poyerekezera ndi kachisi amene Solomoni adamanga, koma Mulungu anati zidzakwaniritsa cholinga chake, ngakhale ndi wochepa poyerekezera ndi kachisi woyamba.

Pamene Yesu anabwera kwa nthawi yoyamba, Herod anali atalemekeza ndi kukongoletsa kachisi yemweyo. Ophunzira ake anamuuza Iye kuti aone m'mene kachisi anali wokongolera. Yesu anati panalibe mwala wina kapena unzake umene sukanagwetsedwa. Kachisi ameneyi anali atakongoletsedwa ndi Herod, koma anagwetsedwa ndi Tito mu 70A.D. Kumangidwa kwa kachisi wachiwiriyu ndikofunika, chifukwa pamene kachisi wachitatu akumangidwa zochitika zomwezo zidzakhalabe.

Haggai 2:4- *"Koma limbika tsopano, Zerubabele, ati Yehova, ulimbikenso Yoswa mwana wa Yohozadaki, mkulu wa ansembe; ndipo mulimbike inu nonse anthu a m'dziko ati Yehova wa makamu:"* Mu vesi limeneli Mulungu anawauza iwo kuti Iye anali nawo ndipo Iye amafuna kachisi amangidwenso, chifukwa amayenera kukonzeredwa choyamba kubwera kwa Ambuye pamene Yesu anabwera ngati mwana mu khola. Amayenera kugwetsedwa patsogolo pake ndi Tito, koma akuyenera kumangidwanso mu tsiku lotsiriza.

Ine ndikufuna ndikuonetsereni chimene chikuyenera kuchitika mu gawo la dziko lapansi pamene kachisi amangidwa. Haggai 2:6-7- *"Pakuti atero Yehova wa makamu: kamodzinso, katsala kanthawi, ndidzagwedeza miyamba ndi dziko lapansi, ndi nyanja ndi mtunda womwe; ndipo ndidzagwedeza amitundu onse ndi zofunika za amitundu onse zidzafika, ndipo ndidzadzaza*

nyumba iyi ndi ulemerero, ati Yehova wa makamu." Uwu ndi uneneri wokhudza nthawi imene kachisi wa Yerusalemu adzamangidwenso mu tsiku lotsiriza ili. Mulungu adzatumiza kugwedeza kwakukulu. Padzakhala nkhondo. Pali mavuto akulu amene akuyembekezera dziko lapansi ili. Pali kugwedeza kwakukulu kukuchitika ndipo zidzafika poipa. Mulungu adzagwedeza mapfuko.

Nyumba imene idzadzaza ndi ulemelero ndi kachisi wachitatu amene adzamangidwa pamene Ambuye mwiniyekha adzakhala mu kachisi ameneyo mu Yerusalemu. Kwa zaka chikwi Yesu adzakhala mu kachisi ameneyo mu Yerusalemu ndipo boma lidzachokera ku Yerusalemu kupita ku dziko lonse lapansi. Mulungu anati, *"Ine ndidzadzaza nyumba iyi ndi ulemerero."* Musadandaule ndi kuchepa kwa nyumba yomangidwayo. Sikanakhala yochepa kwambiri, koma ilibe ulemerero monga yoyamba imene Solomo adamanga. Mulungu adati, "M'maso mwanu siikuoneka chilichonse, koma ndidzamanga wina ndipo ndidzakhala mwa iye." Mulungu adalankhula zimenezo mu nthawi yoti amangidwe kuti padzakhala kugwedeza kwa zinthu zonse.

Haggai 2:8- *"Siliva ndi wanga, golide ndi wanga ati Yehova wa makamu."* Mwakulankhula kwina, ndikanatha kumanga wabwino tsopano, ndi chimene akulankhula. Iye amawauza kuti apitirize ndi kumanga ameneyo, chifukwa amayenera kugwetsedwabe. Haggai 2:9 *"Ulemelero wotsiriza wa nyumba iyi udzaposa woyambawo, ati Yehova wa makamu, ndipo m'malo muno ndidzapatsa mtendere, ati Yehova wamakamu."* Padzakhala mtendere pa dziko, ndipo ulemerero wa nyumba inayo udzaposa ulemerero wa nyumba yakaleyo, mwa kulankhula kwina, kachisi wa mu Mileniamu adzakhala wapamwamba kuposa amene Solomo adamanga.

Tsopano tikupita ku chaputala *chachinai* cha Zakaria, chikutiuza za nthambi ya Azitona, mboni ziwiri. Zakaria 4:1-3- *"Ndipo mthengayo adalankhula nane, anadzanso, nandiutsa ngati munthu woutsidwa mtulo tache. Ndipo anati kwa ine, uona chiyani? Ndipo ndinati, ndaona, taonani, choikapo nyali cha golide yekha yekha, ndi mbale yache pamwamba pache, ndi nyali zache zisanu ndi ziwiri pamenepo, nyalizo zinali ndi misiwe isanu ndi iwiri, ndiyo ya nyalizo zinali pamwamba pache; ndi mitengo iwiri ya azitona pomwepo, wina ku dzanja lamanja la mbaleyo, ndi wina ku dzanja lache lamanzere."* Mitengo iwiri ya azitona ikuimirira mboni ziwiri ku Chivumbulutso 11 pamene kachisi wachitatu akumangidwa.

Zakaria 4:4-6 – "*Ndipo ndinayankha ndi kunena ndi mthenga wakulankhula ndi ine, ndikuti, izi ndi ziyani mbuyanga? Ndipo mthenga wakulankhula ndi ine anayankha nati kwa ine, sudziwa kodi kuti nziani izi? Ndipo ndinati, iai, mbuyanga. Pamenepo anayankha, nanena kwa ine, ndi kuti, awa ndi mau a Yehova kwa Zerubabele, ndi khamu la nkhondo ai, ndi mphamvu ai, koma ndi Mzimu wanga, ati Yehova wa makamu."* Ndi chinachake, ife tikuyenera kuphunzira. Sinkhondo, simphamvu, koma ndi Mzimu wa Ambuye. Mulungu ali nayo ntchito yoti achite. Mulungu ali ndi ntchito ya uzimu kuti apange ndipo iye akuimanga mu nthawi ino ndipo simwa nkhondo ya thupi, si mwa mphamvu ya thupi, koma mwa Mzimu wa Ambuye. Pamene Mulungu akhala okonzeka kuichita, Iye amachita.

Zakaria adafunsa kuti mitengo ya azitona iwiri iyi inali chiyani, koma wam'thenga sanayankhe chifukwa amafuna kuti amuuze chinachake koyamba, ndipo kenako akanamuuza chimene mitengo ya azaitona iwiri inali.

Kumbukirani kuti iwo amabwerera ku dziko kukamanga kachisi. Padzakhala kachisi omangidwa mu masiku otsiriza ndipo takuonetsani inu mu Bukhu la Haggai kuti padzakhala kugwedeza kwakukulu ku Israeli pamene akumangidwa.

Zakaria 4:7- *"Ndiwe yani, phiri lalikulu iwe? Pamaso pa Zerubabele udzasanduka chidikha, ndipo udzatulutsa mwala wa chimbudzi, ndikupfuula, chisomo, chisomo nao."* **Kodi zikutanthauza chiyani? Kachisi anali atagwetsedwa, chimulu chokha chachikulu, chiphiri**

cha zinyalala. Mzimu wa Ambuye unalankhula nuti, *"Ndiwe yani, phiri lalikulu iwe? Pamaso pa Zerubabele udzasanduka chidikha."*

Ife tikanabweretsamo apa chinachake chokhudza Mkwatibwi wa Khristu. Zikuoneka ngati mpingo wagwetsedwa, chimulu chokha chachikulu. Zipembedzo zangopanga chinyansi pa zonse zimene Mulungu wayesera kuchita mu dziko la Amitundu, mu mpingo. Ndi chiphiri chachikulu cha zokugwa. Zikuoneka ngati Bukhu la Machitidwe lagwetsedwa. *"Ndiwe yani, phiri lalikulu iwe?"* Taganizani za funso limenelo. Phiri liti? Ndi pamene kachisi anayatsidwa, chimulu chokha cha zinyalala. Zimaoneka ngati sakanamangidwa ndi chithandizo chimene anali nacho, koma ochepa akhoza kuchita zambiri ngati Mulungu atalowa m'menemo. Akuti, *"Pamaso pa Zerubabele udzasanduka chidikha,"* kutanthauza Iye adzachotsa zinyalala ngakhale kupeza mwala wa chimbudzi, ndi kumanga kachisi wa thupi wachiwiriyo.

Kodi Zerubabele anali ndani? Iye anali mkulu wa Boma, ndipo anali ndi mtima wogwira ntchito. Baibulo likuti ku Nehemia kuti anthu anali ndi lingaliro logwira ntchito. Mulungu akuika mwa Mkwatibwi wa Khristu mtima wogwira ntchito, mtima wotenga malo, mtima onena, "Zonse ndi zotheka kwa onse amene akhulupirira." Ngakhale mwala wapa chimbudzi, mwala wa pangodya, unali penepake mkatikati mwa zinyalala. Mulungu anati, pamaso pa Zerubabele phiri limenelo lidzakhala chidikha. Mwakulankhula kwina, Iye adzachotsa phiri pa njirayi ndipo ngakhale kupeza mwala wa chimbudzi, mwala wa pangodya, ndi kuubweretsa kumapfuula "Chisomo, chisomo, kwa Ambuye." Izi zikulankhula za kachisi wa thupi- koma ine ndikufuna kuonjezerapo mau pa Mpingo.

Mwala wathu wa chimbudzi ukubwera mu nthawi ino. Baibulo likuti mwala umene amisiri omanga nyumba anaukana wasanduka mwala wa pa ngodya. Ndi Yesu Khristu. **Iye akubweranso ku mpingo, ndipo Baibulo likuti chisomo chachikulu chimenecho chidzabwera ku mpingo wa vumbulutso la Yesu Khristu.** [1Petro 1:13]

"Ndiwe yani phiri iwe?" Kodi mukuziona? *"Ndiwe yani chipembedzo? Ndiwe yani?"* Chimulu ichi cha zinyalala cha zipembedzo zidzasanduka chidikha. Mau a Mulungu adzasesa maziko kukhala abwino. Kachisi adzamangidwa, ndipo mwala wa chimbudzi udzaikidwa pa malo ake oyenera.

Zipembedzo zayesetsa kuchita zinthu zambiri, koma sanaupeze mwala wa chimbudzi ndi kuuika pamalo olondola. Iwo akufuna kupanga Bishop kapena kabungwe ka ma dikoni mutu wa mpingo. Bungwe la ma dikoni si mutu wa mpingo. Yesu Khristu ndi mutu wa mpingo.Iye adzalamulira mpingo. Inu mukhoza kukhala nawo madikoni anu, kuvota kwanu kulowa ndi kutuluka, ndi zina zotero, koma pamene muthana nazo kuchita zimenezo ndi pamene Mulungu amayambira.

Apa akuti, *"ndipo iye adzatulutsa mwala wa chimbudzi ndi kupfuula."* Pali chimwemwe potumikira Ambuye. Bukhu la Nehemia likuti chimwemwe cha Ambuye ndi chilimbikitso chanu. Mwala wa pa chimbudzi wabwezeretsedwa. Phiri likupangidwa kukhala chidikha. Maziko achotsedwa ndipo tili pa miyala kuti timange kachisi wa Mulungu wa moyo. Tsopano tibwerere ku kachisi wa thupi. Zakaria 4:8-10 *"Ndipo Mau a Yehova anadza kwa ine, ndi kuti, manja a Zerubabele anaika maziko a nyumba iyi, manja ake omwe adzaitsiriza; ndipo udzadziwa kuti Yehova wa makamu ananditumа kwa inu. Pakuti wapeputsa tsiku la tinthu tating'ono ndani? Pakuti adzakondwera, asanu ndi awiri awa, nadzaona chingwe cholungamitsira chiriri m'mdzanja la Zerubabele, ndiwo maso a Yehova, ayendayenda mwa dziko lonse."*

Ngakhale pamene amamanga khoma, pamene ena mwa iwo nabwerera, chinali chiyambi chaching'ono mpaka ena a iwo anakhumudwitsidwa, koma Mulungu anati amange kachisi;

mangani khoma, mangani nyumba. Si mphamvu, kapena nkhondo, koma ndi Mzimu wanga, atero Mulungu. Ndani amene adzanyoza tsiku la zinthu zazing'ono?

Kenako Zakaria anafunsanso funso lokhudza mitengo iwiri ya azitona. Zakaria 4:11-14- *"Pamenepo ndinayankha, ndinati kwa iye, Mitengo iwiri ya azitona kulamanja ndi kulamanzere kwa choikapo nyali ndi chiyani? Ndipo ndinayankha kachiwiri, ndinati naye, nzotani nthambi ziwiri izi za azitona ziri kutsanula zokha mafuta onga golide mwa misiwe iwiri ya golide? Ndipo anandiyankha, nati, sudziwa kodi kuti mziyani izi? Ndipo ndinati iai, mbuyanga. Pamenepo anati, Awa ndi ana amuna awiri a mafuta oimirira pamaso pa Mbuye wa dziko lonse lapansi."* Mitengo iwiri ya azitona iyi ndi odzozedwa awiri. **Kodi odzozedwa awiri awa ndi ndani? Mose ndi Eliya ndi odzozedwa akulu awiri amene sanakhalepo pa dziko kupatula Yesu Khristu.** Awa ndi odzozedwa awiri amene amakhala pamaso pa Ambuye.

Tiyeni tibwerere ku Chivumbulutso 11 ndipo tione ngati zikumveka. Taonani, panali aneneri awiri pa nthawi yomanga kachisi wachiwiri. Uyu anali kachisi amene anagwetsedwa mu 70A.D. Mulungu anati Iye adzamanga kachisi kachiwiri ndipo ulemerero wa yachiwiriyo udzaposa ulemerero wa yoyambayo, ndipo Iye anati, "Ine ndidzakhala pakati pa iyo ndidzabweretsa mtendere." Kachisi ameneyi adzagwira ntchito mu gawo loyamba la sabata la 70 la Danieli limene lidzayambe pamene kuchita kwa Mulungu ndi Amitundu kutha pokamba za Mulungu kuchita ndi iwo monga mu mibado ya mpingo.

Tiyeni tiwerenge mavesi awa kachiwirinso. Chivumbulutso 11:1- *"Ndipo anandipatsa ine bango ngati ndodo, ndi kuti, tanyamuka, nuyese kachisi wa Mulungu, ndi guwa la msembe, ndi iwo akulambiramo."* Mulungu anaika Mau *"guwa"* m'menemo kuonetsera kuti ndi malo omwewo a kachisi yemweyo, chifukwa ndi thanthwe limene mwana wa nkhosa anaperekedwa msembe mu Yerusalemu.

Palibe njira iliyonse izi zikulankhula za kachisi wa uzimu amene ife tili. Izi zikukamba za kachisi wa thupi amene adzamangidwa ku Yerusalemu. Matupi athu ndi kachisi wauzimu wa Ambuye, koma inu mungatiyeze bwanji, ndi iwo amene amapembedza, ndi guwa? Ndipo inu mungawaike pati aneneri awiriwa ndi kachisi kugwetsedwa ndi amitundu? Palibe njira yoziikira. Chivumbulutso 11:1 chikulakhula za kachisi amene adzamangidwe mu Yerusalemu mu tsiku lotsiriza ili. Iye adzamangidwa.

Otsutsakhristu adzabwera ndikukhala mu kachisi ameneyo pakati pa sabata. Baibulo likutero mu chaputala chachiwiri cha 2 Atesalonika kuti iye adzakhala mu kachisi wa Mulungu ndi kupembedzedwa ngati Mulungu.

Yesu anati ku Yohane 5:43- *"Ndadza ine mu dzina la Atate wanga ndipo simunandilandira Ine; koma akadza wina mu dzina lache la mwini iyeyu mudzamulandira."* Uku kunali kuwauza Ayuda kuti pamene papa abwera ku Yerusalemu ku kachisi ngati karonga wa mtendere adzamulandira iye, koma tsopano Ambuye adzabwera ndi kuyeretsa kachisi.

Chivumbulutso 11:2- *"Ndipo bwalo la kachisi la kunja kwa kachisi ulisiye padera, osaliyesa; pakuti adapatsa ilo kwa amitundu; ndipo mzinda wopatulika adzaupondereza miyezi makumi anai mphambu iwiri."* Apa ndi pamene otsutsakhristu akutenga.

Taonani mitengo iwiri ya azitona. Chivumbulutso 11:3-4- *"Ndipo ndidzalamulira mboni zanga ziwiri, ndipo zidzanenera masiku chikwi chimodzi ndi mazana awiri mphambu makumi asanu ndi limodzi, zovala chiguduli. Izo ndizo mitengo iwiri ya azitona ndi zoikapo nyali ziwiri zakuima pamaso pa Ambuye wa dziko lapansi."* Kodi mukuona chimene chiri tsopano? Pamene kachisi wachiwiri anamangidwa, iye anaona mitengo ya azitona iwiri ndi odzozedwa awiri. Apa, akufotokoza chimene chinali.

Pamene kachisi wachitatu akumangidwa aneneri awiri awa adzaima ku Yerusalemu ndi kunenera. Iwo adzasandutsa madzi magazi ndipo padzakhala nthawi yakugwedeza pamene kachisi uyu adzakhala akumangidwa, koma adzamangidwa kukwaniritsa Mau a Mulungu. Mboni izi ziwiri zidzanenera zaka zitatu ndi theka kapena miyezi makumi anai ndi iwiri. Iwo sikuti adzakhala Mose ndi Eliya apachiyambi, koma adzakhala amuna awiri okhala ndi kudzoza kwa Mose ndi Eliya.

Ndi ndani amene anatseka kumwamba kuti mvula isagwe mu masiku a kunenera kwake kwa zaka zitatu ndi theka? Eliya. Ku Aigupto, ndi ndani amene anasandutsa madzi kukhala magazi? Mose. Mzimu wa Ambuye udzawadzoza iwo komanso kudzoza kumene Mose anali nako ndikudzoza kumene Eliya anali nako.

Vesi 7: *"Ndipo pamene zidatsiriza umboni wao chirombo chokwera kutuluka mphompho chidzachita nazo nkhondo, nichidzazilaka, nichidzazipha izo."*

Papa wa ku Roma akupanga pangano ndi Israeli ndi mafuko ena kumayambirira kwa sabata la 70 la Danieli, koma pakati pa sabata papa akuswa pangano. Pamene iye akuswa pangano lake iye akulamula kuti aphedwe aneneri awiri awa. Palibe munthu amene angawagwire mpakana atatha kupereka umboni wao, chifukwa moto ukutuluka kuchokera mkamwa mwawo ndi kuononga adani awo. Iwo adzalankhula mau achiweruzo, monga Petro anachitira, ndipo adani awo adzafa mpakana Mulungu atathana nawo.

Pokhapokha Mulungu ali ndi china chake ndi iwe kuti uchite, ndipo iwe waitanidwa ndi kudzozedwa ndi kuikidwa kuti uchite chinachake, ndiye mdirekezi sangakuletseni inu. Iye akhoza kukusokonezani ndi kulankhula za inu. Aneneri awa awiri, mosakaika, anali ndi adani ambiri chifukwa anthu anasangalala pamene iwo anaphedwa, koma iwo anali atatsiriza uneneri wao, chirombo, otsutsakhristu, mdierekezi, asanadzuke ndikuwapha iwo. Papa adzalamulira izo.

Vesi 8: *"Ndipo mitembo yao idzakhala pa khwalala la mudzi waukulu, umene utchedwa, ponena zauzimu Sodomu ndi Aigupto, pameneponso Ambuye wao anapachikidwa."*

Kodi Ambuye wathu anapachikidwa kuti? Ku Yerusalemu. Ndi chifukwa chiyani akutchedwa Sodomu ndi Aigupto apa? Zikuonetsera chinthu chimodzi. Pamene anthu anasonkhana kumudzi kwao, ku Israeli, mu tsiku lotsiriza ili iwo anachokera ku pfuko lililonse la Amitundu. Ndipo anabweretsa mizimu iliyonse mizimu yomweyo uko, monga Sodomu ndi Gomora, monga Aigupto, monga dziko lapansi.

Inu mutati muyende mu makwalala a mzinda wa makono wa Tel-Aviv, inu simungasiyanitse ndi mizinda ya Amitundu. **Mizimu ikulowa m'menemo kuchokera ku pfuko lililonse la Amitundu pamene Ayuda akubwerera** kwao **ku Israeli.** Zili monga Sodomu ndi Aigupto. Mulungu ananena kuti zikhale mu njira imeneyi mu tsiku lotsiriza. Ndi m'mene zidzakhalire pamene aneneri awiri adzaphedwa.

Vesi 9: *"Ndipo a mwa anthu ndi mafuko, ndi manenedwe, ndi mitundu apenyera mitembo yao masiku atatu ndi nusu lache, osalora mitembo yao iyikidwe m'manda."*

Vesi 10: *"Ndipo iwo akukhala pa dziko adzakondwerera, nasekerera, nadzatumizirana mitulo; popeza aneneri awa awiri anazunza iwo akukhala pa dziko."*

Kodi mukuona chimene aneneri awiri adzachite? Iwo adzabweretsa Mau a Mulungu. Iwo adzatseka kumwamba kuti mvula isagwe. Iwo adzasandutsa madzi magazi. Iwo adzaitana 144,000 kuti alalikire uthenga osatha ku dziko lonse lapansi. Iwo adzapatsa mpingo wa Chiroma njira yovuta kuyendamo. Iwo udzachita misala, ndipo pamene iwo udzadzuka ndi kupha iwo, anthu adzasangalala ndi izo mpakana adzatumizirana wina ndi mzake mphatso chifukwa iwo

adzaganiza kuti zatha, koma chiweruzo cha Mulungu chikufuna chiyambe kutsanuridwa. *"Tsoka. Tsoka, kwa onse okhala pa dziko lapansi."* **Ili ndi tsoka lachiwiri.**

Vesi 11: *"Ndipo atapita masiku atatu ndi nusu lache mzimu wa moyo wochokera kwa Mulungu unawalowera, ndi kukhala chiriri; ndipo mantha akulu anawagwera iwo akuwapenya."*

Vesi 12: *"Ndipo anamva mau akulu akuchokera kumwamba akunena nao, kwerani kuno. Ndipo anakwera kumka kumwamba mu mtambo; ndipo adani awo anawapenya."*

Iwo mpakana sangawaike m'manda aneneri awiri kwa masiku atatu ndi theka, chifukwa iwo akusangalala kuti afa. Mosakaika, iwo adzati, "Asiyeni iwo akhale pomwepo ndi kuvunda," chifukwa iwo akusangalala ndi kuwaseka iwo, koma akatha masiku atatu ndi theka Mzimu wa Mulungu ulowa mwa iwo ndipo pali kukwatulidwa. Iwo akutengedwa kupita ku mpando wa chifumu wa Mulungu. Izo zikutsiriza chifundo cha Mulungu ndi kutsiriza chisindikizo cha Mulungu. Mngelo anabweretsa chisindikizo mu Yerusalemu ndi kunena kuti *"gwirani mphepo zinai mpakana titasindikiza akapolo a Mulungu pa mphumi pao;"* mu nthawi iyi kusindikizidwa kwatha. Kenako hade watsegulidwa.

Vesi 13: *"Ndipo panthawipo panali chivomerezi chachikulu, ndipo limodzi la magawo khumi a mudzi lidagwa; ndipo anaphedwa m'chivomerezicho anthu zikwi zisanu ndi ziwiri; ndipo otsalawo anakhala a mantha, napatsa ulemelero kwa Mulungu wa mwamba."*

Apa akuti, *"Otsalawo anakhala ndi mantha, napatsa ulemerero kwa Mulungu wa mwamba."* **Koma izi sizikutanthauza kuti iwo analapa machismo awo.** Iwo anangochita mantha mwa kanthawi. Anthu akanatha kunena, "Aneneri awiri amene aja akuyenera kukhala a Mulungu," koma osalapa. Mulungu amatha kuwachititsa anthu mantha nthawi zina, koma sizimachita chilichonse ku miyoyo yawo. Iwo amangopitabe njira zawo. Ayuda a ndale awa adzakhala mu nzere umodzi ndi otsutsakhristu pamene iye akubwera mu kachisi. Iyi ndi nthawi imene iye akuswa pangano ndi kulowa mu kachisi.

Vesi 14: *"Tsoka lachiwiri lachoka; taonani, tsoka lachitatu lidza msanga."*

Kupha aneneri awiri ndi tsoka lachiwiri ndipo pali linanso limodzi loti lichitike. Ili mu chaputala cha khumi ndi chiwiri cha Chivumbulutso, kumene satana waponyedwa kuchoka kumwamba kupita pa dzikolapansi.

Poona m'tsogolo, kodi mukuona kuti kachisi wa thupi adzamangidwa mu Yerusalemu? Iye adzamangidwa. Aneneri awiri adzanenera mu Yerusalemu. Iwo adzakhala ndi mzimu wa Eliya ndi Mose. Iwo adzaphedwa ndi kuikidwa makwalala amzinda kwa masiku atatu ndi theka. Mulungu adzawadzutsa kwa kufa. **Mzimu wa Mulungu udzalowa mwa iwo ndipo iwo adzapita mu Mkwatulo.** Kenako pa nthawi imeneyo padzakhala chivomerezi chachikulu.

Vesi 15-19 likuonetsa nyengo ya nthawi imene ikutsegulidwa mwa kuomba kwa lipenga la chisanu ndi chiwiri. Nyengo ya nthawi imeneyi ikuchitika mpakana ku gawo la chitatu la chiukitsiro choyamba ndi maufumu adziko lapansi ili kusandulika ufumu wa Ambuye Yesu Khristu. Taonani izi pamene tikuwerenga vesi 15-19.

Vesi 15: "*Ndipo mngelo wachisanu ndi chiwiri anaomba, ndipo panakhala mau akulu m'Mwamba, ndi kunena, Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi Khristu wache: ndipo adzachita ufumu kufikira nthawi za nthawi."*

Vesi 16: *"Ndipo akulu makumi awiri mphambu anai akukhala pa maso pa Mulungu pa mipando ya chifumu yawo, anagwa nkhope yao pansi nalambira Mulungu."*

Vesi 17: *"Nati, tikuyamikani, Ambuye Mulungu, wamphamvu zonse, amene muli, ni munali, popeza mwadzitengera mphamvu yanu yaikulu, ndipo mwachita ufumu."*

Vesi 18: *"Ndipo Amitundu anakwiya, ndipo unadza mkwiyo wanu, ndi nthawi ya akufa yakuti aweruzidwe, ndi yakupereka mphotho akapolo anu anenerіwo, ndi oyeramtima, ndi iwo akuopa dzina lanu, ang'ono ndi akulu ndi kuononga iwo akuononga dziko."*

Vesi 19: *"Ndipo anatsegulidwa kachisi wa Mulungu amene ali m'Mwamba; ndipo linaoneka likasa la chipangano chache, m'Kachisi mwache, ndipo panali mphenzi, ndi mau, ndi mabingu, ndi chivomerezi, ndi matalala akulu."*

Vesi 19 likufotokoza vesi 15, m'mene likutionetsera chimene kuomba kwa lipenga la chisanu ndi chiwiri kukuchita. **Kuomba kwa lipenga lachisanu ndi chiwiri kukutsegula malo oyeretsetsa mu kachisi kumwamba, ndi kumene mpando mwa chisomo uli.** Pokhapokha mpando wa chifumu ukugwiritsidwa ntchito, pali mtundu wina wa chisomo pa anthu, koma kuomba kwa lipenga lachisanu ndi chiwiri kukung'amba chophimba mu kachisi ndipo mpando wa chifundo uli poyera. Ine apa ndikunena za choimirira, kuonetsa kuti pamene lipenga lachisanu ndi chiwiri liomba m'bado i-k-u-t-h-a, koma osati monga ngati chala chanu. Zikutsegula nyengo ya nthawi ya kutsanula kwa miliri isanu ndi iwiri ya chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chimodzi.

Lipenga lachisanu ndi chiwiri ili likuomba kuyandikira kumapeto kwa sabata la 70 la Danieli monga uthenga wa 144,000 ukupita kumapeto, kuonetsera kuti sipadzakhalanso chifundo lipenga ili likaomba, mpakana Yesu Khristu atabwera ku dziko ili mu kubwera kwake mu thupi kudzakhala mu kachisi omangidwanso mu Yerusalemu. Apo muli ndi kumasulira kwa chaputala cha khumi ndi chimodzi cha bukhu la Chivumbulutso. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHIWIRI

Vesi 1: *"Ndipo chizindikiro chachikulu chinaoneka m'mwamba; mkazi wovekedwa dzuwa, ndi mwezi ku mapazi ache, ndi pamutu pache korona nyenyezi khumi ndi ziwiri."*

Apa tikuyang'ana mkazi. Iye waima pa mwezi ndipo dzuwa liri pambali pake. Yohane anaona izi pamene iye anayang'ana kumwamba. Izi sizitanthauzira zokha pamene tikupita kuonetsera chimene mkazi ameneyi ali. Korona wa nyenyezi khumi ndi ziwiri akuonetsa kuti mkazi akuimirira pfuko la wanthu. **Mkazi uyu si wina koma pfuko la Israeli.**

Mu chaputala cha chisanu ndi chiwiri cha bukhu ili, ife tinaonetsa pamene 144,000 anasindikizidwa. Ichi si chithunzi cha 144,000, ngakhale kuti 144,000 ndi Ayuda, koma ichi ndi chithunzi cha pfuko lonse la Israeli. Yohane sakuona 144,000 mu chaputala ichi. Chimene Yohane akuona mu vesi loyamba ndi chithunzi cha Israeli mu mileniamu. Kenako kotsatira kwa chaputala ichi, iye akuonetsedwa chimene Israeli akuyenera kudutsamo asanalowe mu mileniamu, kapena mu m'bado wake wa ufumu.

Mu chaputala cha khumi ndi chimodzi taona m'mene kachisi anamangidwira. Kodi mukudziwa chifukwa chiyani anamangidwa? Yesu adzakhala mu kachisi ameneyo mu Yerusalemu, ndipo Israeli adzawala ngati pfuko nambala wani mu mileniamu. Baibulo likuti ku Zakaria kuti kudzakhala Mfumu imodzi ndipo dzina lake lidzakhala M'modzi. Inde, pfuko la Israeli lidzabwezeretsedwanso ndi mafuko khumi ndi awiri m'malo mwao, awa ndi nyenyezi khumi ndi ziwiri mu korona wake. Pfuko la Israeli lidzakhala ulemerero wa dziko lonse mu m'bado wa mileniamu.

Kodi dzuwa likuimirira chiyani? Likuimirira m'bado wa lamulo umene iye wadutsamo. Iye akuima pa mwezi, kuwala kochepa. Mwezi ulibe kuwala kwa iko kokha. Umayenera kutenga kuwala kwache kuchokera ku dzuwa. Lamulo lilibe mphamvu yopulumutsa, koma linali ndi

maulosi amene amalozera nthawi yomwe Israeli adzapita mu m'bado wa ufumu. Yesaya chaputala 11 ndi 65, chikufotokoza za ulemerero wa iye.

Anthu ena amafunsa, "Kodi lamulo siinali choimirira cha m'bado wa chisomo?" Inde, koma pali malemba ena ku Chipangano Chakale amene akufotokoza za Israeli mu m'bado wake wa ufumu kwambiri kusiyana ndi mpingo. Apa pali chifukwa: **Chimene Mulungu adanena za mpingo chinali chinsinsi.** Paulo anati Mulumgu wamuika iye kuti adziwitse chinsinsi cha m'mene Amitundu adzakhalire gawo la thupi limenelo. [Aefeso 3:6]

Ma ulosi amene anapangitsa Israeli kukhala ndi pakati ali ku Chipangano Chakale ndipo ndi woimirira mwezi, kapena m'bado umene iye wadutsamo, iye akuimabe, koma akuima pamaso pa ulemerero wa dzuwa, kuonetsera kuti wadutsa mu m'bado wa lamulo kulowa mu m'bado wa mileniamu. Ulemerero wa dzuwa uli kumeneko. Mafuko onse khumi ndi awiri ali kumeneko, chifukwa pali nyenyezi khumi ndi ziwiri mu korona.

Ku Mateyu chaputala 19, Petro anamuuza Ambuye kuti anali atasiya zonse ndikumutsatira Iye, ndipo amafuna kuti adziwe chimene adzakhale nacho. Tiyeni tiwerenge ichi ku Mateyu 19, kuti muone chimene korona wa nyenyezi khumi ndi ziwiri chili. Anthu ena amakhulupirira kuti ndi uthenga wa atumwi khumi ndi awiri. **Israeli samazindikirika ndi atumwi khumi ndi awiri. Iye amazindikirika ndi mafuko khumi ndi awiri**. Izi zimazindikiritsa pfuko chifukwa cha korona pa mutu pake wokhala ndi nyenyezi khumi ndi ziwiri. Mateyu 19:27-28- *"Pomwepo Petro anayankha, nati kwa Iye, onani ife tinasiya zonse ndi kutsata Inu nanga tsono tidzakhala ndi chiyani? Ndipo Yesu anati kwa iwo, Indetu ndinena kwa inu, kuti inu amene munanditsata ine, mkubadwanso, pamene Mwana wa munthu adzakhala pa chimpando cha ulemerero wache, inunso mudzakhala pa mipando khumi ndi iwiri, kuweruza mafuko khumi ndi awiri a Israeli."*

Pali mipando yachifumu khumi ndi iwiri, ndipo atumwi amenewo akukhala pa mipando khumi ndi iwiri ya chifumu ndi kuweruza mafuko khumi ndi awiri a Israeli. Kotero nyenyezi zikuzindikiritsa mafuko a Israeli. Iwo ali mu korona. Korona akuyenera kuchita ndi Israeli mu thupi, gawo la dziko lapansi. Atumwi amayenera kuchita ndi Uthenga wa Uzimu, Mau a Mulungu.

Mau oti **"kubadwanso"** ku Mateyu 19, akutanthauza *kulenganso ndi kukonzanso*. Ndi dziko kuchepetsedwa anthu. Uyu adzakhala mileniamu pamene iye adzabwereranso ku dziko ndi atumwi khumi ndi awiri akukhala pa mipando khumi ndi iwiri ya chifumu kuweruza mafuko khumi ndi awiri a Israeli. Mwezi pansi pa mapazi ake zikuimirira m'bado wa lamulo umene iye anadutsamo. Iye akuimirira mu ulemerero wa dzuwa, chimene chikutanthauza kuti ali tsopano mu mileniamu mu masomphenya awa.

Kachiwirinso, mundilore ndinene kuti uwu simpingo. Nyenyezi khumi ndi ziwiri sizikuimirira atumwi khumi ndi awiri. **Panali mafuko khumi ndi awiri kale mbuyomo pasanakhale atumwi khumi ndi awiri.** Israeli samadziwika ndi atumwi khumi ndi awiri. Israeli amadziwika ndi mafuko khumi ndi awiri a Israeli.

Vesi 2: *"Ndipo anali ndi pakati; ndipo anapfuula ali nkubala ndi kumva zowawa za kubala."*

Mkazi uyu anali ndi mwana. Iye ali ndi pakati. Kodi iye anabereka ndani? Iye anabereka Yesu Khristu. Ine ndikufuna kuti ndikuonetsereni pfuko ili pamene liri ndi pakati pa maulosi a Mau a Mulungu.

Ku Yesaya 7:14 kuli ulosi; ndipo munali mu pafupifupi 742B.C., n'neneri ananenera kuti pfuko la Israeli lidzabereka Messia, ndipo Messia amayenera kubwera ngati kamwana kakang'ono. Yesaya 7:14-*"Chifukwa chache Ambuye mwini yekha adzakupatsani inu chizindikiro, taonani namwali adzaima, nadzabala mwana wa mwamuna, nadzamutcha dzina*

lache Imanueli." Kodi mukuona ulosi umenewo? Ulosi umenewu ndi wa kwa pfuko la Israeli. Yesaya ananenera kuti pfuko la Israeli lidzabereka mwana wa mwamuna. Chaputala cha chisanu ndi chinai cha Yesaya chikufotokoza zambiri za izi ndikuonetsera kuti mwana uyu adzakhala ndi ulamuliro pa mapewa pake, ndipo sadzachita zimenezo kufikira mileniamu. Yesaya 9:6- *"Pakuti kwa ife mwana wa khanda wabadwa, kwa ife mwana wa mwamuna wapatsidwa; ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lache, ndipo adzamutcha dzina lache Wodabwitsa , Wauphungu, Mulungu wamphamvu, Atate Wosatha, Karonga wa mtendere."* Wabadwa ndi ndani? Mwana, mwana wa mamuna. Taonani m'mene Mesia amayenera kubwerera ku dziko lapansi. Namwali amayenera kuima ndi kubereka mwana. Maulosi amenewa amenenera za Israeli. Kotero namwali Maria mkatikati mwa pfuko la Israeli anabereka Yesu Khristu.

Kodi mukuona m'mene mkazi ameneyu anatengera pakati? Mwa maulosi, Mau a Mulungu. Iye amayenera kubereka chiyani? Mwana wa mwamuna. Iye amayenera kudzakhala chiyani? Mulungu Wamphamvu, Atate wosatha, Karonga wamtendere, Karonga wamtendere. Mwa chidule, Iye ndi Yesu Khristu.

Vesi 3: *"Ndipo chinaoneka chizindikiro china mwamba, taonani chinjoka chofiira, chachikulu, chakukhala nayo mitu isanu ndi iwiri, ndi nyanga khumi, ndi pamutu pake nduwira za chifumu zisanu ndi ziwiri."*

Chirombo chofiira chachikulu ichi chikuonetsera Ufumu wa Chiroma, ndipo chinatsogoleredwa ndi satana njira yonse. Nduwira pa mitu isanu ndi iwiri zikutanthauza kuti maonekedwe onse asanu ndi awiri a boma la Chiroma akuonetseredwa apa. **Chirombo cha chiroma ichi chakhala chikutsutsana ndi Israeli kudutsa mu mbiri yonse.**

Ku Chivumbulutso, chaputala 13, palibe nduwira pa mitu isanu ndi iwiri, kutanthauza kuti sizikudutsa kuchoka mu gawo lina kupita mu gawo lina nthawi iyi, koma kuti chafika kumene chimapita. Ndipo nduwira zili pa nyanga, koma ndi chirombo chomwecho. Yohane adaona mkazi wa pakati akubuula ndi ululu. Kenako, iye adaona chirombo chachikulu chofiira. Awa ndi masomphenya. Kodi mukudziwa kuti chirombo chofiira chimaimirira chiyani? Chikuimirira mdierekezi pamene akudziveka thupi ekha mu ufumu wakatolika wa Chiroma kupyolera mu nyanga khumi za ku Ulaya, maiko aku ulaya, monga adalamulira mu M'bado wa M'dima mbuyomo mu nyengo ya ma B.C. Yohane sakanatha kuona mdierekezi, mdierekezi ndi mzimu. Inu simungathe kumuona mdierekezi pokhapokha atavala thupi yekha mu njira inayake. Iye wakhala akudziveka yekha thupi kwa zaka zikwi zambiri mu kachitidwe aka ka Chiroma. Chirombo "chofiira" chikuimirira mtundu wa chifumu wa mafumu woyamba a mafumu wa Chiroma.

Vesi 4: *"Ndipo mchira wache uguza limodzi la magawo atatu a nyenyezi zamwamba, nuziponya padziko. Ndipo chinjoka chinaimirira pamaso pa mkazi akuti abereke, kuti akabereka icho chikalikwire mwana wache."*

Pamene Yesu anabadwa, ndi ndani amene anayesera kumupha iye? Anali Herodi, mfumu ya Chiroma ya kuYudea amene adapanga lamulo kuti ana onse kuyambira zaka ziwiri ndi kutsikirapo aphedwe kuti ayesere kufunafuna ndi kupha Yesu Khristu. [Mateyu 2:16] Koma Mulungu anatetezera Iye pomutumiza Iye ku Aigupto.

Kodi simukuchiona chirombo chofiira chachikulu chimene chinaima pamaso pa mkazi kuti chiononge mwana wake akangobadwa? Mau a Mulungu amadziyankhira okha. Akuzizindikiritsa kuti chirombo chofiira chimenechi ndi chiyani. Akuzizindikiritsa ndi kuonetsera chimene chinachitika pamene Yesu anabwera kwa nthawi yoyamba. Chirombo chinayesera kumupha Iye.

Yesu sanabadwe kwa Ayuda kuti angokhala mpulumutsi. Iye anabadwa kuti akhale Mfumu yawo. Iye anabadwa kuti awapulumutse ngati pfuko. Ndi njira imene amayang'anira Iye kubwera. Pamene anzeru akum'mawa anabwera ku Betelehemu, iwo sanafunse za mpulumutsi amene akanadzafa pa mtanda. Koma iwo anafunsa, *"Ali kuti Iye amene wabadwa mfumu ya Ayuda*?" Pamene Herodi anamva kuti panali Mfumu imene yabadwa, iye anati mwana ameneyo akuyenera kuthedwa ngati iye akufuna kudzakhala Mfumu. Kotero anatumiza ndi kupha ana onse kuyambira zaka ziwiri kutsika m'munsi.

Chirombo chofiira chachikulu ndi Roma, monga mdierekezi akuziveka yekha mu kachitidwe kupyola mu katolika kwa mibado ya mpingo ngakhale nthawi ya Khristu ndi mu nyengo ya ma B.C.

Vesi 25: *"Ndipo anabala mwana wamwamuna amene adzaweruza mitundu yonse ndi ndodo ya chitsulo: ndipo anakwatulidwa mwana wache amuke kwa Mulungu, ndi ku mpando wa chifumu wache."*

Izi zikuti apa *"iye anabala mwana wa mwamuna, amene adzalamulira,"* gwirani chimenecho, koma Iye sanayambe kulamulira.

Kodi Yesu anabadwa kuti adzakhale ndani? Iye anabadwa kuti adzakhale Mfumu. Zakaria anati, "Mfumu ya dziko lapansi." Koma chinamuchitikira iye ndi chiyani? Ayuda anati "Mpachikeni Iye." Koma ndi ndani amene adampachika Iye? Aroma adamutengera Iye pa phiri la Gologota ndikumukhomera Iye pa mtanda.

Vesi lachisanu likuti, *"Mwana wake anakwatulidwa amuke kwa Mulungu, ndi ku mpando wachifumu Wache."* Yesu analakika ndi kukhala pansi pa mpando wachifumu wa Atate wake ndipo anati, *"Kwa iye amene alakika ndidzampatsa kukhala ndi ine pa mpando wanga wachifumu, monga inenso ndinalakika, ndipo ndinakhala ndi Atate anga pa mpando wake wachifumu."* [Chivumbulutso 3:21]

Iye amene amakhala pa mpando wa chifumu umenewo [Chivumbulutso 4] ndi yemweyo amene anabadwa ngati kamwana kakang'ono ndipo anakwatulidwa kupita ku mpando wachifumu wa Mulungu; ndipo adakali pomwepo. Taonani, Iye anakwatulidwa kupita kwa Mulungu ndi ku mpando Wake wa chifumu. Iye anakhala pa mpando wa Atate wachifumu, Iye ndi Yesu. Israeli anabereka mwana amene amayenera kudzalamulira maiko, koma Iye anakwatulidwa kupita kwa Mulungu ndi pa mpando Wache wachifumu. Chifukwa chiyani? Kuti akhale okhululukira machimo.

Funso likhoza kufunsidwa, "Kodi Iye adzalamulirabe?" Yankho ndi loti inde. **Yesu adzalamulirabe dziko kwa zaka chikwi ndi kukhala pa mpando wake mu nzinda wa Yerusalemu.**

Mkazi yemweyu amene ndi Israeli, amene anabereka mwana wa mwamuna, Mpulumutsi, alinso ndi nthawi ina yaikulu ya chisautso.

Chaputala ichi sichikuchita kwenikweni ndi 144,000 ngakhale kuti 144,000 ndi gawo la pfuko.

China chake chimene ine ndikufuna kuti inu muone ndikufuna kuti inu muone chimene ndi kiyi wa chaputala ichi. **Pakati pa lachisanu ndi vesi la chisanu ndi chimodzi pali pafupifupi nyengo ya zaka zikwi ziwiri.** Ameneyi ndiye kiyi wa chaputala. Taonani kuti iye amene akuyenera kulamulira maiko anakwatulidwa kupita kwa Mulungu ndi mpando wake wachifumu.

Pamene Petro amalalikira mu chaputala chachitatu cha Machitidwe, anati kumwamba kukuyenera kumlandira Yesu kufikira nthawi ya kukonzanso kwa zinthu zonse, kufikira nthawi ya kulenganso, kufikira nthawi ya ulamuliro wa mileniamu itayamba. Mu kusintha, ndi chimene akulankhula.

Akhristu a chiyuda amayang'anira kuti Yesu abwera ngati munthu, ngati Mfumu, kukwaniritsa ulosi waku Chipangano Chakale, ndipo anamufunsa iye mu chaputala choyamba cha Machitidwe, pamene iye amapita, ngati Iye akanatha mu nthawi imeneyo kubwezeretsa ufumu ku Israeli. Iye anawauza iwo kuti sikunapatsidwe kwa iwo kudziwa nthawi kapena nyengo, koma kuti adzalandira mphamvu Mzimu Woyera atabwera pa iwo ndikuti adzakhala mboni za Iye mu Yerusalemu, Yudea, Samaria, ndi madera onse a dziko lapansi asanabwere Iye kukhala pa mpando Wake pa dziko lapansi.

Vesi 6: *"Ndipo mkazi anathawira ku chipululu, kumene ali nayo mbuto yokonzeratu ndi Mulungu, kuti kumeneko akamdyetse masiku chikwi chimodzi ndimazana awiri mphambu makumi asanu ndi limodzi."*

Amenewo ndi masiku 1260, miyezi 42, kapena zaka zitatu ndi theka. Mkazi yemweyu amene anabereka mwana wa mamuna tsiku lina adzathawa kupita ku chipululu kuthawa pa maso pa chirombo. **Kumbukirani kuti uwu simpingo. Mpingo sukuyenera kuthawa pa maso pa chirombo. Iye akupita mu Mkwatulo.**

Pakati pa sabata, aneneri awiri atatha kunenera, 144,000 atanyamuka ku Israeli kupita kuzungulira dziko lapansi ndi kulalikira uthenga, mkazi yemweyu adzayenera kuthawa pamaso pa chirombo.

Aneneri awiri akuuza mkazi uyu koti apite ndi cholinga choti akhale otetezedwa munthawi ya nyengo ya chisautso chachikulu kuti alowe mu mileniamu ngati pfuko. Izi zikuphatikiza akazi, ana, amuna, amuna okalamba, ana ang'ono, ndi onse. Ndi gawo la anthu a ku Israeli amene Mulungu adzagwiritse ntchito kuchulukitsa pfuko la Israeli mu mileniamu.

Mkazi yemweyo, pfuko lomwelo, limene linabereka Messia, limene linabereka Yesu Khristu, akuoneka kuthawa kulowa mu chipululu kuthawa pa maso pa chirombo.

Ine ndikufuna ndikuonetsereni inu m'mene mkazi akuthawira mu Israeli pamaso pa chirombo. Iye akuyenda pa mapiko awiri a chiombankhanga chachikulu. Mulungu anatulutsa ana a Israeli ku Aigupto ndi chiombankhanga. Ndi ndani amene anaombola ana a Israeli kutuluka mu Aigupto? Mose. Eksodo 19:4 akuti Iye anawatulutsa pa mapiko a chiombankhanga. Mkazi uyu akuyenera kuthawa. Ndi mu masiku otsiriza, pamene otsutsakhristu adzaswa pangano ndipo Ayuda amene adamva aneneri akudziwa nthawi yotuluka.

Vesi 7: *"Ndipo munali nkhondo mwamba Mikayeli ndi angelo ake akuchita nkhondo ndi chinjoka; chinjokanso ndi angelo ake chinachita nkhondo?"*

Vesi 8: *"Ndipo sichinalakika, ndipo sanapezekanso malo awo m'mwamba?"*

Mikayeli ndi angelo ake akumenyana ndi mdierekezi ndi angelo ake tsopano. Satana anali ataluza nkhondo imodzi mbuyomo asanabwere kwa Adamu m'munda mwa Edeni, chifukwa iye anali kale kalonga wakugwa mbuyomo. [Yesaya 14:12-15, Ezekieli 28:13-15] Iye analuza nkhondo imeneyo m'bado wa mbiri isanayambe, koma apa, satana walowa mwa anthu komanso kudzera mu kachitidwe. Ndi kachitidwe ka Chiroma. Zipembedzo zonse zidzathera mu kachitidwe ka chipembedzo ndipo Roma adzakhala mutu wa chimenecho.

Nkhondo imeneyi ikuchitika kumwamba tsopano. Mikayeli akumenya lero. Ichi ndi chifukwa chake Israeli akutenga malo komanso chifukwa chimene iwo sangawononge Israeli. Israeli adzaima. **Pamene ndiona mkazi uyu akuima pa mwezi komanso kuvekedwa dzuwa, zikutanthauza kuti iye adzaikidwa mu mileniamu.** Izi zikuonetsera kuti satana akuluza nkhondo. Mikayeli ndi angelo ake anamenyana ndi chinjoka ndi angelo ake. Chinjoka ndi angelo ake *"sanalakike, malo ake sanapezekanso mwamba."* Izi zikutanthauza kuti alibenso mpata ku

gawo la kumwamba. Satana akudziwa kuti iye waponyedwa pa dziko lapansi, ndipo akudziwa kuti kwake kwatha. Izi zikuchitika pakati pa sabata.

Vesi 9: *"Ndipo chinaponyedwa pansi chinjoka chachikulu, njoka yokalambayo, iye wotchedwa mdierekezi ndi satana, wonyenga wa dziko lonse; chinaponyedwa pansi ku dziko, ndi angelo ake anaponyedwa naye pamodzi."*

Vesi 10: *"Ndipo ndinamva mau akulu m'mwamba, nanena, tsopano zafika chipulumutso, ndi mphamvu, ndi ufumu za Mulungu wathu, ndi ulamuliro wa Khristu wache; pakuti wagwetsedwa wonenera wa abale athu, wakuwanenera pamaso pa Mulungu wathu usana ndi usiku."*

Satana wagwetsedwa kuchoka ku gawo la kumwamba ndipo sipatenga nthawi mpakana atathedwa. Taonani liu ili kuchokera kumwamba. Pamene satana akugwetsedwa kuchokera ku gawo la kumwamba akuti, *"wonenera wa abale athu wagwetsedwa."* Izi zikukamba za pfuko la Israeli. Amitundu akhala akunenera Israel, ndikumugwetsa, ndipo zikuchulukirabe nthawi zonse, koma onenera adzagwetsedwa ku dziko. Satana wagwetsedwa kuchokera kumwamba.

Vesi 11: *"Ndipo iwo anamulaka iye chifukwa cha mwazi wa Mwana wa nkhosa, ndi chifukwa cha mau a umboni wao; ndipo sanakonda moyo wao kungakhale kufikira imfa."*

Kodi iwo anamlaka mdierekezi motani? Ndi mwazi wa Mwana wa nkhosa, ndi mau a umboni wao. Kodi mau a umboni wao ndi chiyani? Ndi lamulo la ku Chipangano Chakale limene iwo adagwiritsitsa chiyambire pamene Mulungu adamupatsa Mose.

Ayuda woona a chi Orthodox adzapereka moyo wao chifukwa cha Mau a Mulungu mu nthawi imeneyo, chifukwa otsutsakhristu adzayamba kampeni ya udani motsutsana ndi Ayuda. Iye adzapha anamwali opusa ndi oyeramtima ena amene adzamva Ayuda 144,000 alaliki amene adzapangitsa iwo kuswa bungwe la chipembedzo. Baibulo likuti, *"iwo sanakonde miyoyo yawo mpakana imfa,"* chimene chikutanthauza kuti iwo anafa chifukwa cha kaimidwe kawo pa Mau.

Vesi 12:- *"Chifukwa chache kondwerani, miyamba inu, ndi inu akukhala momwemo. Tsoka mtunda ndi nyanja, chifukwa mdierekezi watsikira kwa inu, wokhala nao udani waukulu, podziwa kuti kumtsatira kanthawi."*

Ili ndi tsoka lachitatu. Satana wagwetsedwa ndipo ndi womasulidwa padziko. *"Tsoka kwa okhala pa dziko,"* pa chifukwa choti satana wabwera. Pamene iye waponyedwa padziko akudziwa kuti iye wachotsedwa ku gawo la kumwamba. Baibulo likuti ali ndi mkwiyo waukulu. Iye akudziwa kuti wangotsala ndi zaka zitatu ndi theka kuti achite chimene akufuna kuchita, tsopano akuyambitsa kampeni ya udani. Iye akupha, ndipo padzakhala chisawawa pa dziko lonse lapansi. Baibulo likuti padzakhala nthawi ya mavuto ndipo ikutchedwa "mavuto a Yakobo." Inde, pali nthawi ya m'dima imodzinso imene Israeli adzadutsemo. Chisindikizo cha chisanu ndi chitatu chikuti minjiro yoyera inapatsidwa kwa iwo, ndipo zanenedwa kwa iwo kuti adikire kwa kanthawi pang'ono mpakana abale awo ndi akapolo anzawo ataphedwanso ngati iwo. Izi zikukwaniritsa gawo lachiwiri la chisindikizo chachisanu.

Vesi 13: *"Ndipo pamene chinjoka chinaona kuti chinaponyedwa pansi kudziko chinazunza mkazi amene adabala mwana wamamuna."*

Mkazi uti amene iye akumuzunza? Israeli. Israeli anali mkazi amene adabweretsa mwana wa mamuna. Sunali mpingo, anali Israeli. Mpingo wapita mu nthawi iyi, kotero chirombo chikanazunza bwanji mkazi ngati mkazi akanakhala mpingo?

Inu simungamupange mkazi mu vesi loyamba kukhala mpingo, ndiye ndikumupanga amene chirombo chikuzunza mu vesi la khumi ndi chitatu kukhala mkazi wina. Ndi mkazi yemweyo. Ndi Israeli. Israeli ndi amene anabereka mwana wa mwamuna. Israeli ndi amene anabereka mpulumutsi, ndipo chirombo chimadziwa zimenezo.

Pamene aneneri amenewo awiri akunenera mu nthawi ya zaka zitatu ndi theka zoyambirira za masabata 70 a Danieli, iwo adzauza pfuko la Israeli kuti pamene awona pangano likusweka achoke mu dziko.

Kumbukirani apa, kuti pamene Yerusalemu anagwetsedwa mu 70 A.D. ndipo Aroma analowa ndi kutseka mzinda, panali ulosi utakhala pamenepo. Unali woti, *"pamene mudzaona mzinda wa Yerusalemu utazingidwa, inu amene muli mu mzinda ndi kumiraga tulukani ndi kupita kumapiri."* [Luka 21:20-24] Izi zinachitika pamene Tito adaononga Yerusalemu. Asilikali a nkhondo anali chizindikiro chimene chinati, "Tulukani mu dziko ndi kupita ku mapiri."

Apa pali mkazi, Israeli, Ayuda amene Mulungu adzagwiritsa ntchito kuchepetsa anthu mu dziko. Pa nthawi imene m'dziko pangano liswedwa ndipo chinjoka chagwetsedwa pa dziko ndi kuyamba kupha, mkazi uyu ali ndi mapiko awiri a chiombankhanga; iwo ali ndi uthenga wa aneneri awiri. Taonani mkazi kuchoka ku dziko. Pa nthawi iyi, Mulungu watulutsa kale ndi kuika amuna 144,000 kuti alalikire uthenga osatha umenewo mu nyengo ya chisautso.

Tsopano taonani gulu lina ili lopangidwa ndi amuna, akazi ndi ana amene atenga uthenga wa aneneri. Taonani vesi lotsatira.

Vesi 14: *"Ndipo anampatsa mkazi mapiko awiri a chiombankhanga chachikulu, kuti akaulukire ku chipululu, ku mbuto yache, kumene adyetsedwako nthawi, ndi zinthawi, ndi nusu la nthawi, osapenya nkhope ya chinjoka."*

Kumbukirani ku Eksodo, pamene akunena kuti Mulungu anatulutsa Israeli ku Aigupto pa mapiko a chiombankhanga. Mkazi uyu anapatsidwa mapiko awiri a chiombankhanga chachikulu. Angati? Awiri. Aneneri awiri. Iye anapatsidwa mapiko awiri a chiombankhanga chachikulu kuti akathe kuuluka kupita ku chipululu, ku malo ake, kumene akadyetsedwe kwa kanthawi [chaka chimodzi], ndi nthawi [zaka ziwiri], ndi nusu la nthawi, [theka la chaka], kuchoka pa nkhope ya chinjoka. Izi zikupanga zaka zitatu ndi theka.

Aneneri awiri adzadziwa, koma pali malo penapake ndipo Mulungu akudziwa pamene ali. Kwinakwake Mulungu adzatsegula pfuko ndi kulora Ayuda amenewo kulowa ndi kuwasamalira mu gawo lotsiriza la sabata la 70 la Danieli.

Iwo anabisidwa mu maiko osiyanasiyana mu chisautso cha Hitler, ndipo Mulungu adawatetezera iwo. Mulungu anawapulumutsa kudutsa mu zisautso zimenezo. Pamene Hitler amafuna kupha muyuda aliyense, Mulungu anawapulumutsa.

Mkazi ameneyi [iwo amene Mulungu adzawagwiritsa ntchito kuchepetsa anthu a pfuko la Israeli] ali ndi malo ake apadera kumene akupita. Ndi kuti? Mulungu akudziwa ndipo aneneri awiri adzadziwa. Zikuganiziridwa kukhala U.S.A ndi Canada.

Vesi 15: *"Ndipo inalavulira mkamwa mwache, potsata mkazi, madzi ngati mtsinje, kuti akakokoleredwe mkazi nao."*

Madzi amenewa ndi gulu la nkhondo la papa, asilikali a Chiroma. Pamene iye akutumiza iwo kwa mkazi ameneyi, mdierekezi adzazindikira kuti pali gulu lalikulu la anthu osowa mu Israeli, koma apita kale.

Padzakhala nthawi ya mtendere, ndipo chirombo [papa] adzawapatsa iwo ufulu mu zaka zoyambirira zitatu ndi theka mpakana mdierekezi atagwetsedwa ndipo iye adzalusa. Pamene iye adzalusa mkazi adzakhala atapita kale. Iye watuluka kale mu Israeli, ndipo papa adzatumiza magulu a nkhondo kunja ndi kuyesera kumufufuza iye, ndipo nthawi yonse adzakhala akupha anamwali opusa ndi oyeramtima ena amene adzatsale pano, ndi kupha akhristu onse amene angakhale ndi Mau a Mulungu.

Ife tikuona mu chaputala cha khumi ndi chisanu cha Chivumbulutso, iwo amene anaima pa nyanja ya mandala. Ndi iwo amene abwera kudutsa mu moto wa chisautso kufika ku

mpando wachifumu, koma mkazi ali kwinakwake otetezedwa pa dziko, ndipo iye adzapita mu ulamuliro wa mileniamu ngati anthu mu thupi.

Vesi 16: *"Ndipo dziko linathandiza mkaziyo, ndi dziko linatsegula mkamwa mwache, nilinameza madzi a mtsinje amene chinjoka chinalabvula m'kamwa mwache."*

Vesi ili silikutanthauza kuti chivomerezi chachikulu chidzameza magulu ankhondo a papa. Zikungotanthauza kuti magulu a nkhondo sakupeza mkazi, monga m'mene magulu a Hitler sanathe kuononga Ayuda amene anabisidwa mu mafuko osiyanasiyana mu nthawi ya nkhondo yachiwiri ya dziko lonse. Pamene mdierekezi mwa papa anazindikira kuti ankhondo ake sangaononge mkazi [Israeli], vesi 17 ikukwaniritsidwa.

Vesi 17: *"Ndipo chinjoka chinakwiya ndi mkazi, nichinachoka kumka, kuchita nkhondo ndi otsala a mbewu yache, amene asunga malamulo a Mulungu, nakhala nao umboni wa Yesu."*

Chinjoka chinakwiya, kapena kuchita misala pa mkazi chifukwa chidaona kuti iye wathawa. Pamene chinjoka chidaona kuti nkazi wathawa icho chidachita misala moti chidangoyamba kupha aliyense amene amalankhula za Mulungu. *"Ndipo anapita kuchita nkhondo ndi otsala a mbewu yake,* ***amene anasunga malamulo a Mulungu, ndi kukhala ndi umboni wa Yesu Khristu."*** **Zikutanthauza chiyani? Zikutanthauza onse awiri Ayuda ndi Amitundu.**

Kodi Amitundu akanakhala bwanji mbewu ya mkazi Israeli? Iwo anabwera ndikukhala gawo la pangano latsopano limene Mulungu adapangana ndi Israeli. Zinali kudzera mwa Khristu, mbewu ya Abrahamu, mwa lonjezo. Pamene chinjoka chikupita, chikupha anamwali opusa, ndi onse amene alephera kulowa mu Mkwatulo, ndi aliyense otchula dzina la Mulungu.

Kodi mukuchiona chaputala cha khumi ndi chiwiri cha Chivumbulutso? Kodi mkaziyo ndi ndani amene adabweretsa mwana wa mamuna? Israeli. Chinjoka chinali yani? Anali mdierekezi pamene iye analowa yekha mu Ufumu wa Aroma. Kodi ndi mkazi uti amene anathawira ku chipululu? Ndi Ayuda amene adamva uthenga wa aneneri awiri, ndi kuthawa dziko la Israeli chinjoka chisanawaphe iwo.

Ayuda awa amene adzapita ku chipululu akuyenera kupita ku mileniamu ngati anthu ku thupi. Mkazi uyu amene adathawira ku chipululu sadzalandira thupi la ulemerero. Iye akuyenera kubereka pfuko ku thupi pa dziko mu nthawi ya mileniamu. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHA KHUMI NDI CHITATU

Vesi 1: *"Ndipo ndinaimirira pa mchenga wa nyanja, ndipo ndinaona chirombo chiri nkutuluka m'nyanja, chakukhala nazo nyanga khumi, ndi mitu isanu ndi iwiri, ndi pa nyanga zache nduwira zachifumu khumi ndi pamitu pache maina a mwano."*

Pamene ife tikuyamba chaputala ichi, ine ndikufuna inu kuti muone kuti nduwira zachifumu zinali pa nyanga zache, osati pa mitu yache. Chirombo ichi ndi chomwecho Danieli adachiona ndichomwecho timaphunzira mu chaputala cha khumi ndi chiwiri cha buku ili. Taonani pa nyanga zache, panali nduwira zachifumu khumi. Zimenezo zikuimirira mafumu khumi kuzindikiritsa mosiyana pamene akupanga mphamvu kwa chirombo, kumeneko ndi ku madzulo kwa Ulaya mu gawo lochuluka.

Kodi mitu ndi chiyani? Roma wadutsa mu nyengo zisanu ndi ziwiri zosiyanasiyana za ulamuliro. **Imeneyo ndi mitu isanu ndi iwiri.** Dzina la mwano pa mitu isanu ndi iwiri ndi dzina la mwano limene olamulira a ufumu wa Chiroma amatchulidwa.

Vesi 2: *"Ndipo chirombo ndinachionacho chinafanana ndi nyalugwe, ndi mapazi ache ngati mapazi a fisi, pakamwa pache ngati pakamwa pa mkango; ndipo chinjoka chinampatsa iye mphamvu yache, ndi mpando wachifumu wache, ndi ulamuliro waukulu"*

Vesi loyamba ndi lachiwiri likuonetsa chirombo cha Chiroma ichi chili mu mphamvu zonse, ngakhale mochuluka kwambiri kusiyana ndi mu M'bado wa M'dima. Apa ali ndi anthu ambiri, madera ambiri, chuma chambiri ndi mphamvu zambiri za nkhondo. Yohane akuonetsedwa izi koyamba. Kenako akuonetsedwa m'mene chirombo ichi chinatengera mphamvu iyi, monga chaputala chotsiriza chikuonetsera.

Iyi ndi nthawi yoyamba chirombo ichi chikuzindikiritsidwa monga chonchi. Kodi mukudziwa kuti chirombo ichi ndi chiyani? **Ndi mdierekezi kuonekera mu kachitidwe.** Apa, izi zikuonetsera chirombo monga palibe malo ena aliwonse mu Chivumbulutso akumuonetsera iye. Thupi lake lili ngati la nyalugwe, mapazi ake ngati a fisi, ndi pakamwa pake ngati mkango. Pali cholinga pochionetsera icho ngati choncho mu gawo lake lotsiriza. Mulungu azipanga izo kudziwika kwa ife tsopano.

Tiyeni titsegule ku Danieli 7 ndipo ife tidzapeza chifukwa chake zili chonchi. Pamene zifika mumaonekedwe awa ndi gawo lotsiriza la mphamvu ya chirombo ya Amitundu, ndi chifukwa chake chikuzindikirika monga mu mibadwo ina yonse

Pamene tikuwerenga ku Danieli, chaputala chachisanu ndi chiwiri, taonani zirombo zinai zikutuluka nyanja ndipo zinali zosiyana wina ndi nzache.

Danieli 7:4- *"Choyamba chinanga mkango, chinali nawo mapiko a chiombankhanga, ndinapenyera mpaka mthenga zache zinathothoka, nichinakwezeka kudziko, ndikuimitsidwa ndi mapazi awiri ngati munthu, nichinapatsidwa mtima wa munthu"* Ife tikudziwa chimene chirombo choyamba chinali, ufumu wa Babulo wolamulidwa ndi Nebuchadnezzar. Danieli 7:5 *"Ndipo taonani chirombo china chachiwiri chakunga chimbalangondo chinatundumuka mbali imodzi; ndi mkamwa mwache munali nthiti zitatu pakati pa mano ache; ndipo anatero nacho, nyamuka lusira nyama zambiri."* Uwu ndi ufumu wa Medo-Peresi. Mthiti mkamwa mwache zikuonetsera kuti wapeza chinachake choti adye. Icho chinameza ufumu wa Babulo. Danieli 7:6 *"Pambuyo pache ndinapenya ndikuona china ngati nyalugwe, chinali nawo mapiko anai a nkhuku pa msana pache, chirombocho chinali nayonso mitu inai nichinapatsidwa ulamuliro."* Uwu ndi ufumu wa Greece pansi pa Alexander Wankulu. Kumbukirani kuti chirombo ichi ku Chivumbulutso 13 chili ndi thupi ngati nyalugwe. Izi zikuonetsa ufumu wa Greece. Madera omwewo amene Alexander amalamulira adzapanga gawo la chirombo chotsiriza mu nthawi yotsiriza.

Greece adzachita ubale ndi kachitidwe ka chirombo ka ku Ulaya, koma Greece sim'modzi wa nyanga khumi. Zidzakhala nyanja zomwezo zimene zinali pa chirombo chisanavulazidwe. Adzakhala madera omwewo akumadzulo kwa Ulaya, chifukwa ndi Ufumu waChiroma Wakale kubwezeretsedwa. Pokhudza za dera lirilonse, zikhoza kupitirira khumi chifukwa zasweka kwambiri, komanso, adzakhala Madera omwewo.

Potsiriza penipeni, chirombo ichi chikubweranso ndikutenga madera onsewa a zirombo zitatu zinazi ndikuzipanga izo chimodzi. Ufumu wa Greece unali wachitatu kulamulira ndipo sunakhalepo m'modzi wa nyanga khumi za kumadzulo kwa Ulaya.

Danieli 7:7 *"Pambuyo pache ndinaona m'masomphenya a usiku, ndikuona chirombo chachinai, choopsa ndi chochititsa mantha, ndi champhamvu choposa, chinali nawo mano akulu a chitsulo, chinalusa ndi kuphyanya ndi kupondereza chotsala ndi mapazi ache, chinasiyana ndi zirombo zonse zidachitsogolera, ndipo chinali ndi nyanga khumi."* Taonani chirombo ichi chokha chili ndi nyanga khumi, koma kachitidwe ka chirombo aka kadzakhudza zirombo zitatu

zonse zimene zikulankhulidwa ku Danieli, chaputala chachisanu ndi chiwiri. Iye amawabweretsa iwo ku pangano ndi iye kuti iye akalamulire dziko la uneneri.

Danieli 7:8 *"Ndinali kulingalira za nyangazi, taonani, pakati pa izo panaphuka nyanja ina, ndiyo yain'gono; patsogolo pake zitatu za nyanga zoyambazi zinazulidwa ndi mizu yomwe; ndipo taonani, m'nyanga m'menemo munali maso ngati maso a munthu, ndi pakamwa pali kunena zazikuru."* Nyanga yayin'gono ndi papa amene amalamulira mphamvu ya chipembedzo. Izi sizinapange nyanga khumi ndi imodzi pa chirombo, chifukwa **inali mphamvu ya uzimu imene inadzuka**.

Kudulidwa kwa nyanga zitatu zikutanthauza kuti mafumu atatu amene adapanga kachitidwe ka chirombo adzaswa malamulo la papa mu M'bado wa M'dima, ndipo papa adzawachotsa pa mpando. Ndipo adzawabwezeretsa iwo akatha kulapa ndi kulambira iye. Kotero tikuona chirombo mu nthawi yotsiriza chiri ndi **nyanga khumi zomwezo.**

Danieli 7:11 *"Pamenepo ndinapenyera chifukwa cha phokoso la mau akuru lidanena nyangayi; ndinapenyera mpaka adachipha chirombochi, ndi kuononga mtembo wache, ndikuupereka utenthedwe ndi moto."* Kodi mukuona chidzachitika ndi chirombo cha Chiromachi? Iye adzaonongedwa ndipo thupi lake lidzaotchedwa.

Danieli 7:12 *"Ndipo zirombo zotsalazo anazichotsera ulamuliro wao, koma anatalikitsa moyo wao, ukhalenso nyengo ndi nthawi."* Kodi akutanthawuza chiyani pamene akuti, *"anazichotsera ulamuliro wao."* Anthu a ku Greece salinso ndi ulamuliro waukulu. Sangadzukenso. Koma *"anatalikitsa moyo wao, ukhalenso nyengo ndi nthawi."* Chifukwa chiyani? Padakali anthu mudera limenelo [Anthu a ku Greece]. Mzimu womwewo, mzimu wa Babulo, pansi pa Nebuchadnezzer umene unakopa ufumu umenewo udakali pomwepo, koma sudzakhalanso ndi mphamvu. Mzimu womwewo wa Medo-Peresi udakali komweko. Taonani kuti ulamuliro wawo unatengedwa, koma miyoyo yawo inatalikitsidwa kwa nyengo ndi nthawi. Ine ndikufuna ndikuonetsereni pamene moyo uli tsopano.

Tiyeni tiwerenge Chivumbulutso 13:2 kachiwirinso. *"Ndipo chirombo ndinachionacho chinafanana ndi nyalugwe, ndi mapazi ache ngati mapazi a fisi, ndi pakamwa pache ngati pakamwa pa mkango; ndipo chinjoka chinampatsa iye mphamvu yache, ndi mpando wa chifumu wache, ndi ulamuliro waukulu."* Ufumu wa Greece unali ngati **nyalugwe.** Ufumu wa Medo-Peresi unali ngati **fisi.** Ufumu wa Babulo unali ngati wa **mkango.** Zirombo zitatu zoyambirira zinamezedwa ndi chirombo chachinai chokhala ndi mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi. Izi zikuimirira chidzalo cha zirombo zinai zimene Danieli adaona mu masomphenya ake, ngakhale pa nthawi imene Danieli anachiona, chirombo chinali mutu umodzi okha, koma chakula mu kudutsa kwa nthawi mpakana chili ndi mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga nkhumi mu nthawi yotsiriza. Ili ndi gawo lotsiriza la ufumu wa Chiroma, pamene Roma wameza mphamvu zoyambirira zitatu za chirombo kuziyanjanitsa mu kachitidwe ka chirombo, ndi papa kukhala mutu wa chinthu chonsecho..., mphamvu zonse zinai mu chirombo chimodzi chimene ndi kubwerezetsedwa kwa ufumu wa Chiroma.

"Ndipo chinjoka chinampatsa iye mphamvu yache, ndi mpando wachifumu wache, ndi ulamuliro wache waukulu." Koma apa tikuona chiyani? Wotsutsakhristu akupanga pangano ndi ambiri pa chiyambi pa sabata la 70 la Danieli, ndipo akufikanso ndikutenga mafuko onsewo ndikuwabweretsa mkatimo ndi pangano. Chimene chinapanga mphamvu zinai za Amitundu zidzathera mumutu wa Chiroma, komano sadzaikanso nyanga ina. Mafuko khumi a ku Ulaya adzakhala omwewo.

Padzabwera chinachake chimene chidzagwedeza dziko la pansi. Pamene kugwedeza kudzatha ndi utsi kutha, mphamvu ya Chiroma idzakhala pomwepo, nyanga khumi

zidzakhala pa chirombo, ndipo papa adzalowamo ndi kupanga pangano ndi ambiri ngati karonga wa mtendere. Kenako mudzaona chirombo chitapangidwa, monga chaonetseredwa ku Chivumbulutso 13. Ichi ndi chaputala chokhacho mu Baibulo chimene chikuonetsera monga chonchi. Papa ameneyi adzalamulira ndi ndodo yachitsulo nthawi ya zaka zitatu ndi theka za sabata la 70 la Danieli. Kodi iye akutenga bwanji mpando ndi ulamuliro waukulu? Mdierekezi akumpatsa iye.

Vesi 3: *"Ndipo umodzi wa mitu yache unakhala ngati unalasidwa kufikira imfa; ndipo bala lake la kuimfa linapola; ndipo dziko lonse linazizwa potsata chirombocho."*

Vesi loyamba ndi lachiwiri likumuonetsa iye atachira kwathunthu ndi wamphamvu kusiyana ndi m'mene analiri poyamba. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye anafikira ndikulowetsa anthu ena, komanso madera. Izi zinawabweretsa pansi pa pangano. Kenako Yohane anaona m'mene anavulazidwira, ndipo kenako kuchiritsidwa asanafike pamenepa.

Yohane adaona imodzi ya mitu yake pamene inavulazidwa ku imfa. Kodi kuvulazidwa kwa mutu wache kunali chiyani? Mu M'bado wa M'dima, papa anatenga mphamvu za ulaliki pa nyanja khumi komanso dziko la uneneri limene anaswa ndipo mafuko amayenera kuchita chimene iye amanena, makamaka maiko a ku Ulaya.

Cha mu 1500, Martini Lutera wa ku Germany anatuluka mu mpingo wa katolika wa Chiroma ndi kuyamba kulalikira, "Olungama adzakhala ndi moyo ndi chikhulupiriro." Ndipo Germany amagwirizana ndi Marten Lutera, ndipo kunali kukonzanso. Izi zinaswa mphamvu ya mpingo wachirombo ichi ndi chibala chakuimfa. Kenako kunabwera Knox, Calvin ndi ena otero, molunjika ndi lupanga la mzimu, aliyense kutengako kagawo pa mutu wotsiriza wa chirombo pamene chimalamulidwa ndi mpingo wa Chiroma.

Gawo lotsiriza la ulamuliro wa Chiroma unali mpingo ndi boma kugwira ntchito limodzi. Anali mafuko khumi ndi papa kumakoka zingwe ndikumawafotokozera chochita. Pamene Martini Lutera anatenga lupanga la uthenga ndikuchilasa, chinakhala pafupifupi kufa. Mwauzimu, chinaluza mphamvu yake. Mpingo komanso dziko zinayamba kutuluka mu M'bado wa Mdima.

Mdierekezi anali ndi zaka chikwi zolamura pa dziko. Iwo analowa mu M'bado wa M'dima akumayatsa ma kandulo ndipo anatulukamo chomwecho. Iwo analowa mu M'bado wa M'dima mu ngolo anatulakamo chimodzimodzi. Mafumu akulu akulu onse a pa dziko, masiku a M'bado wa M'dima asanafike anagwa ndipo kunalibe. Zinali ngati kuti dziko likubwerera mbuyo, koma pamene kuwala kwa uthenga kunayamba kuwala, anthu anayamba kutukuka ku katundu ndi zina. Baibulo likuti, *"Yambani mwafuna ufumu wa Mulungu ndi chilungamo Chake,"* ndipo zinthu zonse zathupi za moyo uwu zidzaonjezeredwa pa inu. Ikani Mulungu ndi ufumu wake koyamba ndipo zonse zidzakhala bwino.

Papa anali ndi mphamvube pa mafuko ena. Koma, kodi mukudziwa chimene Napoleon Bonaparte wa ku France anachita? Iye anatumiza General Bertier kuti achotse pampando papa mu 1887. Iye anamutengera ku France, kumuika mu ndende, ndipo iye anafera komweko [Taonani: Mfundo zambiri izi zachokera ku zolemba za Raymond Jackson]. Kodi mukudziwa kuti chinali chiyani? Uku kunali kuvulaza mwa nkhondo. Izo zinathetsa mphamvu ya upapa. Panali kulankhula ku Ulaya kuti, "Upapa wafa ndipo palibe wina aliyense amene adzatukula dzanja kuthandizapo." Kodi mukutha kuona bala lakuimfa pa mutu otsiriza? Mpingo wa katolika wa Chiroma pafupifupi udafa. Zitatha izi papa sanayeserenso kuika mphamvu zambiri, ndipo papa samamvekanso mpakana Nkhondo Yoyamba ya Dziko Lonse. Kenako anayambanso kuzionetsera. Bala la kuimfa linayamba kuchira. Yohane anaona chirombo ichi chikulandira bala lalikulu lakuimfa, koma linachiritsidwa ndipo dziko lonse linadabwa nacho.

Ine ndikufuna kutenga chinthu chinanso chimodzi muvesi 3. Likuti, *"ndipo dziko lonse linazizwa potsata chirombocho."* Palikusiyana pa mawu oti "lonse" pamene mukulankhula za iwo mwauneneri, kusiyana ndi pamene mukulankhula za iwo mu thupi. Nthawi zambiri pamene tikulankhula za "dziko lonse" tikulankhula za anthu onse pa dzikolapansi, koma pamene Yohane analemba zimenezo "dziko lonse linazizwa potsata chirombo," iye amalemba za dziko lapansi la uneneri. Kutali Kum'mawa sadzamvera zimene papa akulankhula. China, Veit, Nam, Tibeti, Cambodia ndi onse maiko a Kutali Kum'mawa sadzakhuzidwa kwambiri ndi kachitidwe kachirombo. Choncho, pamene inu muti "lonse" inu mumawatengera mawu kutali ndi kuima nao. Izi zikukamba za dziko lapansi la uneneri, osati maiko a Kutali Kum'mawa ndi ma Orientals. Chivumbulutso16, chikuchita ndi zimenezo pamene chikukamba za mtsinje wa Filate kuphwa kupanga njira kwa mafumu a kum'mawa. Iwo satengapo gawo lililonse kufikira nkhondo ya Armagedo. Roma sadzatha kumukhutiritsa China. Iwo adzakhala pansi pa hamala ndi chikwakwa. Onse Kutali Kum'mawa adzakhala pansi pa chikominisiti.

Vesi 4: *"Ndipo amalambila chinjoka, chifukwa chinachipatsa ulamuliro chirombocho; ndipo analambira chirombo ndikunena, Afanana ndi chirombo ndani? Ndipo akhoza ndani kugwira nkhondo nacho?"*

Pamene Baibulo likuti iwo analambira chinjoka, **zikutanthauza kuti, iwo analambira m'derekezi kudzera mu kachitidwe ka mpingo.** Ambiri lero, mu maonekedwe onyenga, akupembedza m'dierekezi kudzera mu mpingo.

Anthu adzanyengedwa kwambiri moti iwo adzati, "Ndani angafanane ndi chirombo ichi? Ichi ndi chinthu chachikulu chomwe sichinakhalepo." Chifukwa chiyani? Chifukwa icho chidzalumikiza pamodzi zipembedzo zonse .Icho chidzalumikiza ankhondo onse a dziko la Kumadzulo ndi Chapakati Kum'mawa. Iwo adzati, "Palibe aliyense amene angachite nkhondo ndi ichi. Palibe aliyense angagonjetse ichi. Ichi ndi chinthu chachikulu chimene sichinakhalepo. Iye ndi Mulungu." Koma ndi m'dierekezi, Baibulo likuti m'dierekezi anamupatsa iye mpando, mphavu yake, ndi ulamuliro wake, ndipo anapembedza m'dierekezi, nati, "Ndani amene angakhoze kuchita nkhondo ndi chirombo?"

Vesi 5: *"Ndipo anachipatsa icho m'kamwa molankhula zazikuru ndi zamwano, ndipo anachipatsa ulamuliro wa kutero miyezi makumi anai ndi iwiri"*

Papa, amene ndi wolankhulira wa kachitidwe ka m'dierekezi akulankhula zinthu zazikulu ndi zamwano. Kodi mwano ndi chiyani? Ndikutenga udindo wabodza. Iye simunthu woti mudzichita naye mantha. Iye akubwera ngati "wolowelera." Iye akubwera mkatimo mwamtendere, **ndipo mwano wake sungakhale wotemberera monga mukhoza kuganiza. Simtundu umenewo wa mwano. Iye amafuna ulamuliro umene ndi Mulungu yekha amene alinawo.**

Gawo lotsiriza la vesi ili likuti mphamvu zinapatsidwa kwa iye kuti apitirize miyezi makumi anai ndi iwiri. Zimenezo ndi zaka zitatu ndi theka kapena gawo lotsiriza la sabata la 70 a Danieli. Sabata la 70 ili la Danieli ndi nyengo ya zaka zisanu ndi ziwiri, ndipo mu gawo lotsiriza m'dierekezi akuyenera kulamulira mwa ufulu. Zinapatsidwa kwa iye **"kuti apitirize"** kutanthauza- iye akuyambira pamene analekera m'mene analandira bala la ku imfa cham'ma 1500. Iye akuchitanso chomwecho pamene achira.

Vesi 6: *"Ndipo chinatsegula pakamwa pache kukanena zamwano pa Mulungu, kuchitira mwano Dzina Lake, ndi chihema Chache, ndi iwo akukhala mwamba."*

"Kuchitira mwano dzina lache," zikutanthauza kuti iye akuchita zinthu mu dzina la Mulungu chimene ndi chosiyana ndi mau a Mulungu. Baibulo likuti pakubwera tsiku limene iwo adzakuphani kuganiza kuti akuchita chifuniro cha Mulungu mwakulankhula kwina, iye alibe ulemu pa Yesu kapena oyera mtima ake.

Vesi 7: *"Ndipo anachipatsa icho kuchita nkhondo ndi oyera mtima, ndi kuwalaka; ndipo anachipatsa icho ulamuliro wapafuko liri lonse, ndi anthu, ndi manenedwe, ndi mitundu."*

Ichi chikuti *"anachipatsa icho kuchita nkhondo ndi oyera mtima, ndi kuwalaka."* Chifukwa chiyani? Iwo amalephera kukonzekera kulowa mu Mkwatulo. Inu muli nawo mwai wokonzekera ndi kulowa mu Mkwatulo, koma mukamasewera ndi Mulungu, kumazipusitsa, osakonzekera, ndiye kwapatsidwa kwa chirombo kuchita nkhondo ndi kugonjetsa inu, ndi kukuphani inu mu nthawi imeneyo. Mulungu akukupatsani inu mpata lero. Iye akuomba lipenga. **Lipenga** [lauthenga] **ili limene Mulungu akuomba, silodzidzimutsa. Ilo lili ndi mau omveka chifukwa likuomba mogwilizana ndi mau a Mulungu. Iwo** [utumiki usanu] **amene akuomba lipenga ali mu kamvekedwe, kamodzi ndi iye amene analemba nyimbo.**

Gawo lotsiriza la vesi ili likuti, *"ndipo anachipatsa icho ulamuliro wa pa pfuko liri lonse ndi anthu, ndi manenedwe, ndi mitundu."* Ndipo kenanso, inu mutenge mau oti "liri lonse" kenano muime. Pamene mau oti "lililonse" atha mu uneneri, inu muime pamenepo apo ai malemba akutherani. Inu mudzakhala ndi otsutsa khristu kulamulira China ndi maiko ena a Kutali Kum'mawa, ndipo pamene mutero inu mudzakhala ndi Mau a Mulungu mosokonezeka moti simungathenso kuziika pamodzi.

Vesi 8: *"Ndipo adzachilambira onse akukhala padziko, amene dzina lawo silinalembedwa m'buku la moyo la Mwana wa nkhosa, wophedwa kuyambira makhazikidwe a dziko la pansi."*

Apa pali nthawi ina pamene tikuona dziko "lirilonse." Komanso, inu mukhoza kuima. Aliyense atati apembedze chirombo sipakanakhala anthu odzachulukitsa dziko mu mileniamu. Tengani mau oti "lirilonse" ndikuwasiya pamene malemba akuwasiya, koma dziko lonse la uneneri ndi dziko lotukuka, tikatero maiko onse a Kumadzulo, Kum'mawa Chapakati, adzakhudzidwa.

Padzakhala anthu ena opatulidwa mu mafuko onse amene sadzakakamizidwa kupembedza chirombo. Iwo sadzakhala ndi kubadwa kwatsopano, koma iwo adzakhala anthu ndithu ndipo Mulungu adzawalora iwo kulowa mu ulamuliro wa mileniamu. Mateyu 25 akuti, iwo sadzaweruzidwa pankhani yoti anali abwino kwa abale kapena ayi.

Vesi 9: *"Ngati wina ali nalo khutu amve."* Ophunzira anamufunsa Yesu nthawi ina chifukwa chiyani amalankhula kwa khamu mu mafanizo. Yesu anati, *"Chifukwa sikunapatsidwe kwa iwo kudziwa zinsinsi za ufumu wa Mulungu, koma kwa inu zapatsidwa."* Kodi inu mulinalo khutu? Kodi mukhoza kumva chimene Mulungu a kunena?

Vesi 10: *"Ngati munthu alinga kundende adzamuka; munthu akapha ndi lupanga ayenera iye kuphedwa ndi lupanga. Pano pali chipiriro ndi chikhulupiliro cha oyera mtima."*

Vesi la khumi, likuonetsera kuti chirombo cha Chiroma ichi chidzaweruzidwa ndi machimo ache. Chivumbulutso chaputala 16 mpaka 20, chikuonetsera izi bwinobwino. Komanso, vesi ili likuonetsera kuti oyeramtima akuchisautso ndi Ayuda amene anaima ndi mau adzakhala okhulupirika ngakhale mu nthawi ya m'dima.

Chirombo cha mwana wa nkhosa

Chirombo cha mwana wa nkhosa ichi chimene chikutuluka pansi chikutanthauza, dera la anthu ochepa, limene ndi U.S.A, ndipo chimadziwika ku Ulaya ngati fuko la kuchipululu. Zimakhulupiridwanso kuti ndi "chipululu" kumene mkazi wa ku Chivumbulutso chaputala chakhumi ndi chiwiri akuthawira kuti atetezedwe. Pamene, chirombo cha ku Ulaya chimene chikutuluka pansi pa nyanja chikutanthauza malo awanthu ochuluka kwambiri, monga Chivumbulutso chaputala 17:1&15 likuonetsera.

Tsopano, ine ndikufuna ndifotokoze chirombo cha mwana wankhosa ndi m'mene iye akubwezeretsera chirombo cha Chiroma ku mphamvu mutsiku lotsiriza ili.

Vesi 11 *"Ndipo ndinaona chirombo china chiri kutuluka pansi; ndipo chinali nazo nyanga ziwiri ngati mwana wa nkhosa, ndipo chinalankhula ngati chinjoka."*

Vesi 12: *"Ndipo chichita ulamuliro wonse wa chirombo choyamba pamaso pache. Ndipo chilambiritsa dziko ndi iwo akukhala momwemo chirombo choyamba, chimene bala lache la kuimfa lidapola."*

Chirombo choyamba chinatuluka nyanja, koma chirombo cha chiwiri chinatuluka mudziko, ndipo **ndi United States of America.** Iye anali ngati mwana wa nkhosa ndipo anakhalabe mwana wa nkhosa mpakana ku mapeto. Kenako akuyamba kulankhula ngati chinjoka ndikunyenga dziko lonse la pansi popanga dziko lonse lapansi kupembedza chirombo choyamba chimene iye akuchichiritsa, monga zafotokozeredwa mu gawo lotsiriza la chaputala ichi.

Chirombo cha chiwiri ichi chimene chinatuluka padziko chimene chili ndi nyanga ziwiri ngati mwana wa nkhosa ndipo chikulankhula ngati chinjoka ndi **"iye"** amene akulankhulidwa kuchokera mu vesi 11 mpaka vesi 15

"Iye" muvesi 16 mpaka 18, ndi chirombo chimene vesi 1 mpaka 10 akulankhula ndipo ndi chithunzi cha mu nthawi yotsiriza ya chirombo cha ku Ulaya. Mavesi 11 mpaka 15 ndi mavesi okhawo mu chaputala ichi amene akukhudzana ndi U.S.A. [chirombo cha mwana wa nkhosa]. Tsopano chifukwa choti tikuzimvetsa izi, kotsalira kwa chaputala ndi kosavuta kumvetsa.

Mwana wa nkhosa uyu ali ndi nyanga ziwiri, izi ndi mphamvu za boma la chitsamunda ndi mphamvu za ulaliki wa Bungwe la Mipingo Padziko lonse, komanso zipani ziwiri za ndale zaku U.S.A., ndipo pali Chiprotestanti ndi Chikatolika .Chirombo cha mwana wa nkhosa ichi chilibe nduwira pa nyanga zache monga chirombo cha ku Ulaya. Nduwira zimaonetsera ufumu. Izi zikutanthauza kuti nyanga ziwiri ziribe maonekedwe osiyana kupatula kaonekedwe kachirombo ichi chonse. Iye akulankhula ngati chinjoka mu tsiku ili lotsiriza.

Tayang'anani mu vesi 12 *"iye"* [U.S.A.], akuonetsera mphamvu zache, monga iye akhala akuchitira, ndipo makamaka Nkhondo ya Chiwiri ya Dzikolonse ikadali mkati komanso itatha, iye akupanga dziko kupembedza chirombo choyamba chimene bala lache la kuimfa lidapola. Iye sanayambepo afunsa wina wake kumupembedza iye, koma fano [Bungwe la Mipingo Padzikolonse ku U.S.A.] ikufuna kupembedzedwa. Vesi 15 ikuonetsera ichi. Mphamvuyo ndi yankhondo komanso ulaliki. Kotero chirombo cha mwana wa nkhosa ichi chikuchiza chirombo cha ku Ulaya chimene Mpingo wa Katolika wakwera mu sabata la 70 la Danieli. Ine ndikuonetserani inu m'mene izi zonse zikugwirana palimodzi mu lotsatira la chaputala ichi.

Tayang'anani kuti *"iye"* [U.S.A.] kubwezeretsedwa ndi kupanga chirombo choyamba ichi kuchira mu chipembedzo ndi ndale.

Nkhondo Yachiwiri ya Dzikolonse isanayambe, nyanga khumi zinasakaniza mbewu zawo pamodzi kuyesa kugwirana pamodzi. Mafumu olemekezeka anakwatira ana awo amuna ndi akazi pamodzi kuyesera kupanga umodzi. Iwo anayesera kupanga mafuko khumiwo pamodzi, koma mumasomphenya ake, Danieli anati sidzidzakhala, chifukwa zinali gawo lina chitsulo ndi gawo lina dothi ndipo kuti sizikanatha kulumikizana pamodzi. Ichi ndi chifukwa chache Nkhondo Yoyamba ya Dzikolonse inabuka; sizikanatha kugwirana. Kenako kunabwera Nkhondo Yachiwiri ya Dzikolonse. Panthawi iyi United States anayamba kukula mu mphamvu. Pamene Nkhondo Yachiwiri ya Dzikolonse inatha, Ulaya anakhala mu bwinja. Iwo anaphurika mu chuma.

Panali anthu amene anakhala mu Germany amene anatenga ndalama zawo ku golosale mu wiribara kuti agule zaku golosale. Kuchepa mphamvu kwa ndalama, ndipo ndalama inatha mphamvu. Ndinawerengapo pena pamene munthu amagwira ntchito mwezi onse ndikungokhala ndi ndalama zongokwanira kugula butter. Kuchepa mphamvu kwa ndalama kunafika ndipo osati Germany ekha, koma Ulaya yense.

Wabwezeretsa ndani? **U.S.A wakhuthulira mabilioni a ma dollar mu maiko aku Ulaya ndikuwathandiza kupanga NATO kuti awateteze iwo, makamaka kupyolera mwa asilikali athu amene akukhala ku Ulaya. Inde, U.S.A. watetezera ulaya ndi kukhuthulira mabilion ama dollar m'menemo ndi kubwezeretsa chirombo ichi.** Ndi chimene dongosolo la Marshall linaliri. Linali kumanga Ulaya, ndipo zinatheka kwambiri.

Tayang'anani, kuti chirombo choyamba chili ndi nyanga khumi, United States uyu chirombo cha mwana wa nkhosa chokhala ndi nyanga ziwiri chimene chinatuluka padziko, chinabwezeretsa chirombo choyamba. Nkhondo Yachiwiri ya Dzikolonse itatha, ndipo mpakana pano, tili ndi magulu ankhondo zikwi zikwi amene ali Kumadzulo wa Ulaya kutetezera kuti Russia angalowe ndi kulanda; koma ndikuuzeni chinachake; Russia ndi chongoopsezera chabe. Russia sadzalamulura mafuko a Kumpoto kwa Ulaya.

Pali Bukhu [Baibulo] ife tikhoza kuwerenga ndi kupeza chimene chidzachitike. Ndi papa amene adzakole nthambo ndi kulamulira kumpoto ulaya ndi dziko la uneneri. Russia adzagonjetsedwa malingana ndi Ezekieli chaputala 38 ndi 39, mudziko la Israeli. Chikominisiti cha Russia chidzalephera. Chatha tsopano. Chilichonse chili m'malo ake kuti sabata la 70 la Danieli liyambe.

Gawo la chipembedzo, ndale, nkhondo, ndi chuma la chirombo lakwaniritsidwa. United States wabwezeretsa kale zimenezo.

Tayang'anani kuti bala la kuimfa lachiritsidwa osati nkhondo yokha, koma chipembedzo. Mpingo wa Katolika uli ndi mpamvunso. Nkhondo Yoyamba ya Dziko lonse itatha, maiko anayamba kutumiza akazembe ku Vatikani. Chinali chiyani? Kunali kumuzindikira papa, chifukwa akudziwa kuti akulamurira ma millioni a anthu, ndipo ngati papa angawakomere mtima pa zimene angachite, ndiye iwo apeza ufulu ndi anthu kupyolera madalitso apapa.

Vesi 13: "*Ndipo* [chirombo cha mwana wa nkhosa] *chichita zizindikiro zazikulu, kutinso chitsitse moto uchokere m' mwamba nugwe pa dziko, pamaso pa anthu"*

Vesi 14 "*Ndipo chisokeretsa iwo akukhala padziko ndizizindikiro zimene anachipatsa mphamvu ya kuzichita pamaso pa chirombo* [chirombo chaku Ulaya] *ndi kunena kwa iwo akukhala pa dziko, kuti apange fano la chirombocho, chimene chinali nalo bala la lupanga nichinakhalanso ndi moyo."*

Izi ndi zimene Yohane adaona mu masompenya ake. Izi zikuimirira mabomba amene U.S.A. anagwetsa. Mu masomphenya ache, Yohane adaona moto ukugwa kuchokera kumwamba, koma zenizeni zake zinali mabomba ndi ma rocket. Akuti "*Ndipo chichita zizindikiro zazikulu, kutinso chitsitse moto uchokere kumwamba."* Kenako akuti iye "*chisokeretsa iwo amene akukhala pa dziko ndi zizindikiro zimene anachipatsa mphamvu ya kuzichita."* Kodi zodabwitsa zotani? **Zodabwitsa za sayansi ndi zodabwitsa za luso**. Kodi mukudziwa kuti chokonzedwa chirichonse chimene chapindulira mtundu wa anthu mumasiku ano, mpakana zaka zochepa zapitazo, zinapangidwa ku United States? Zinatero. Komanso chirombo ichi cha mwana wa nkhosa pa vesi 14 chi kuliuza dziko lapansi kuti lipange fano la chirombo chimene chinavulara ndi lupanga ndipo chili ndi moyo .Limeneri ndi Bungwe la Mipingo Padzikolonse (W.C.C.) limene linayambira ku United States. **Ndi Bungwe la Mipingo Padziko lonse kusandulika fano la mpingo wa Aroma.**

Vesi 15: *"Ndipo anachipatsa mphamvu ya kupatsa fano la chirombo mpweya, kutinso fano la chirombo lilankhule, nilichite kuti onse osalirambira fano la chirombo aphedwe."*

Fano limenelo lapangidwa, koma moyo sunapatsidwe kwa ilo. Chorombo cha mwana wa nkhosa sichinauzire mpweya mu fanolo. **Opanga malamulo a mu United States adzauzira mpweya wa moyo mwa icho pamene achipatsa mphamvu ndi ulamuliro kunena chimene mpingo uli ndi chimene suli.** Ndipo pamene chichita, nthawi iyi mitima ya anthu izakhala italimba mpakana adzapha amene sadzagwirizana ndi icho. Inu mukhoza kufotokoza kuti iwo akulimbitsa mitima motsutsana ndi Mau a Mulungu tsopano.

Padzafika nthawi imene oyera mtima aku chisautso adzaphedwa, chifukwa iwo adzatsutsana ndi chivundi cha mipingo ya zipembedzo. Zina mwa kachitidwe ka mpingo akunena kuti ziribwino azitumiki kukhala amuna ogonana, komanso kukwatirana anthu a ziwalo zofanana. Zafika pa uchimo otani? Tithokoze Mulungu anthu ochepa akuchoka mu mabungwe amenewa .Onse amene ali ndi Mulungu atulukamo. Mukuona m'mene zikufikira ponyansa? Padzakhala winawake amene adzatsutsana ndi chisokonekero ndipo pamene achita iwo adzamupha nthawi imeneyo. Nthawi imeneyo sim'bado wina kutali koma ili pafupi.

Pa nthawi imene fano la chirombo lidzayamba kulankhula ndi ulamuliro, kachitidwe ka Katolika wa Chiroma kadzakhala kakulamulira chirombo cha Kumadzulo kwa Ulaya; chifukwa Chivumbulutso chaputala 17 chikuonetsera hule wankulu atakwera pa chirombo. Papa adzakhala akulamulira chuma cha dziko la uneneri, makamaka malo amene awonetseredwa kumayambiriro kwa chaputala ichi, ngakhale kuti sidzidzakhudza madera okhawa, chifukwa chilemba cha chirombo chidzakhudza dziko lonse lapansi; makamaka pamene papa aphwanya pangano lache ndipo akufuna ulemu onse ukhale kwa iye, ndipo iye akuyamba kupha onse amene adzakane kumulambira iye. Izi sizikhudza Kutali Kum'mawa. Izi zafotokozedwa mu chaputala cha khumi ndi chisanu ndi chimodzi cha bukhu ili.

Chirombo choyamba mu chaputala ichi kunali kupanga mbiri ndi kukwaniritsa malemba mbuyo Amerika asanapezedwe. U.S.A. atabwezeretsa chirombo ichi, U.S.A. adzatenganso mpando pokhudza zochitika za dziko lapansi, pamene chirombo cha ku Ulaya chidzayamba kulankhulanso. Pamene chilemba cha chirombo chikhazikidwanso ndi chirombo cha ku Ulaya ichi kupyolera mwa papa ndi Mpingo wa ku Roma, fano [Bungwe la Mipingo pa Dzikolonse] lidzalandira mphamvu kupyolera mwa chirombo cha mwana wa nkhosa ndi kukhala cha nkhanza basi monga Mpingo wa ku Roma ndikupha iwo onse amene sadzapembedza chirombo kapena fano lache. U.S.A. adzakhudzidwanso ndi kachitidwe ka chuma ka chirombo cha ku Ulaya ndi papa wa ku Roma, koma mwa muyeso otani izi sizidzaziwika mpakana nthawi imeneyo itakwana. **Koma ife tikhoza kutsimikiza izi kuti ana akazi a hule wamkulu adzatsanzira mai,** kuonetsera kuti ali mbewu ya otsutsa khristu, ndipo iwo adzapha akhristu a ku chisautso pamodzi ndi mai wawo hule, pakuti onse ali ana ake akazi mahule. Ndikutsimikiza kuti inu tsopano mukuona chirombo cha mwana wa nkhosa ndi fano lake pokha pokha ngati mwachititsidwa khungu ndi satana, Mulungu wa dziko lino. Tsopano kubwerera kwa chirombo cha ku Ulaya chimene chabwezeretsedwa ndi chirombo cha mwana wa nkhosa.

Chirombo chotuluka Nyanja

Vesi 16: *"Ndipo chichita kuti onse ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka, ndi mfulu ndi akapolo, alandire chirembo pa dzanja lao ndi pamphumi pao."*

Vesi 17: "*Ndi kuti munthu sangakhoze kugula kapena kugulitsa, koma iye yekha wokhala nacho chilembo, ndilo dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lache."*

Vesi 17 likuti, "*munthu sangakhoze kugula ndi kugulitsa, koma iye yekha wokhala nacho chilemba, ndilo dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lache."* Ku Ulaya, pali chirombo chobwezetsedwa. Icho ndichoti chizindikiritsidwe pamodzi ndi kachitidwe konseka ka chipembedzo. Kumbukirani apa, izi sizikukhudzana ndi Kutali Kum'mawa komanso ma Orientals. Komanso, tichita ndi zimenezo muchaputala 16.

Limodzi la masiku amenewa, dollar komanso ndalama zina za mu dziko la uneneri sizikhala ndi mphamvu mochuluka, chifukwa zonse zikupita ku ma computer a magetsi mu masiku otsiriza. Pofika mu nthawi pakati pa sabata, chinthu ichi chidzakhala chitakhazikika ndi kumangika mpakana poti inu simungathe kugula kapena kugulitsa pokhapokha inu mutayenda mu zimenezo. Ngakhale ma credit cards monga ife tikuzidziwira za izo posachedwapa zitha.

Ngakhale pali njira zambiri zosagwira ndalama kuti mupange business zimene zikuyesedwa, nthawi siinakwane kuti kachitidwe kameneka kagwiritsidwe ntchito pobweretsa chilemba cha chirombo mu kukwaniritsidwa kwake. Izi zikuonetsera kuti pamene nthawi ifika chirichonse chidzakhala chokonzeka ndipo papa wa ku Roma [wotsutsa-Khristu] adzatenga ulamuliro wa izo.

Vesi 18: "*Pano pali nzeru. Iye wakukhala nacho chidziwitso awerenge chiwerengero cha chirombocho; pakuti chiwerengero chache ndi cha munthu; ndipo chiwerengero chache ndicho mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi asanu ndi limodzi kudza zisanu ndi chimodzi."*

Mwa kulankhula kwina, 666 ndi nambala. Kodi nambalayi ili ndi chochita chotani ndi izo? Ndi nambala imene kachitidwe ka chirombo kadzagwiritsa ntchito popanga madongosolo ake. Kachitidwe kachirombo sikadzagwiritsa ntchito manambala, kamene kakuchitika lero. Iwo amene akukonza dongosolo limenelo sakudziwa kuti zidzagwiritsidwa ntchito ndi papa kukakamiza dziko la uneneri kulambira mdierekezi kupyolera mu mphamvu ya udindo wa papa, pamene nthawi imeneyo ifika pafupi mtsogolomu.

Ine ndikufuna kubweretsa chinthu chimodzi kuti ndionetsere poyera tanthauzo la vesi 18 la chaputala ichi pamene chikukamba za nambala ya munthu. **Vicarius Filii Dei pa nduwira ya papa, pamene ziphwanyidwa mu kalembedwe ka Chiroma zimakwana 666. Izi zikuonetsera ife amene adzakhale oyang'anira mu nthawi imeneyo.** [Yang'anani chojambula pansipa]

Pofika pakati pa sabata, chilembo cha chirombo ndi nambala la dzina lache zidzakhala chenicheni, koma sizidzadziwika bwinobwino mpakana nthawi imeneyo itafika, imene ili pafupi.

Chidziwitso: Izi sizikupanga kuganiza kuti mutaye ma khadi anu a ndalama kapena makhadi achuma amene mukhoza kukhala nawo pa nthawi ino. **Dziko lapansi silidzakakamizidwa kutenga chilemba mpakana** pakati pa sabata la 70 la Danieli. Mkwatibwi wakwatulidwa kale kuchoka pano pa nthawi imene chilemba cha chirombo chikukamizidwa pa anthu.

Kudutsa kupitirira apa sikungakhale bwino pa nthawi ino, komanso kwenikweni zosafunika kwa Mkwatibwi amene achoka pa dziko choipa ichi chisanachitike, kotero tiyeni tizisiye pomwepa, chifukwa ife Mpingo Woona, sitidzakhala pano pamene **chilemba chenicheni** cha chirombo chikuchitika. Izi ndi chenjezo kwa inu kuti mumve chimene mzimu akunena kwa mipingo. Amen.

VICARIUS FILII DEI

V – 5	F – 0	D - 500
I – 1	I – 1	E - 0
C -100	L – 50	I - 1
A – 0	I - 1	
R – 0	I - 1	
I – 1		
U – 5*		
S – 0	Total= 666	

- Mu Latin U ndi wofanana ndi V, kupanga izo kukwanira bwinobwino 666.